# CHIYANI CHIDZAPANGITSE ANTHU OCHURUKITSA KUSALOWA KUMWAMBA

## LIMODZI LA MAGAWO ATATU LA ANGELO A LUSIFARA LINAGWETSEDWA KUCHOKERA KUMWAMBA

### *KUBATIZIDWA KWA CHIKUNJA M'CHIKHRISTU*

Perpetua anakanitsitsa kupereke nsembe ku mafano monga linafunira lamulo m'nthawiyo; akanatero, kukanakhala kupeputsa chikhulupiriro chake ndi kumkana Khristu. Anauza omkakamizawo kuti iye ayenera kumvera Mulungu. Patatsala masiku owerengeka kuti anyongedwe, m'ndendemo anaponyedwanso mai wina wachichepere, Felisitasi, yemwenso anakanitsitsa kunyoza Khristu. Tsiku lakunyongedwa, m'mwezi wa March, A.D. 205 litakwana, awiriwo anatengedwera kumalo a za masewero, naponyedwa ku nyama zolusa zomwe zinawakhadzulana.

Tikakhulupirika, tidzakomana nao awiriwa kumwamba. Tiyenera kuchifera choonadi cha m'Baibulo; Tiyenera kumfera Yesu; tiyenera kuufera moyo wosatha. Choopsya kalelo, ndi leronso, ndi chakuti anthu ambiri chikhristu chao ndi cha pakamwa, osakhala cha chikhulupiriro chozikika m'Mau a Mulungu. Kupembedza mafano m'nthawi ya Perpetua ndi Felisitasi kunali kotere:

"Nsembe za tsiku ndi tsiku kwa Isis…zinazikika mwa m'Roma aliyense. Pamakhala mautumiki awiri; ansembe m'miyinjiro-yoyera, ndi othandizira ao, amachita mautumiki a nsembe m'mawa ndi madzulo. Mapemphero ndi nsembe za m'mawa zinali zogwira mtima…" - Samuel Dill, "Roman Society from Nero to Marcus Aurelius," pp. 577-578. London Macmillan, 1904.

Zomwe amachita opembedza mafanowo, sizikusiyana ndi mautumiki a "nsembe ya misa" a chi-Katolika, kupatula kuti kalelo zinali ku milungu yachikunja osatchulamo Mulungu woona; pamene lero zikukhala ngati za Chikhristu pomatchulamo dzina la Khristu. Asanalowetsedwe m'chikhristu ndi Aroma asanawatengere, mautumiki achikunjawa anachitidwa ku Maiko Akum'mawa ndi m'Aigupto. Pokanitsitsa za chikunjazi, akhristu ozikika m'chiphunzitso cha m'Baibulo anaponyedwa m'Malo osungiramo nyama zolusa zomwe zinawapha.

Wakhala uli mwambi kuti miseu yonse imafikitsa ku Romu, komwe pang'ono pang'ono, akhristu oyambirira analora machitidwe ambiri achikunja. Machitidwewo anaphatikiza amuna kumeta mpala (Lev. 21:5; Deut. 14:1) monga njira imodzi yolemekezera mulungu wa Dzuwa ndiponso kuwaza madzi m'malo mwa ubatizo womiza wa m'Bukhu Lopatulika (Machitidwe 8:35-38; Aroma 6:3-5). Kuchokera ku India Aroma anatengera moyo wodzisankha [wauchiyenda-yekha] ndi kapembedzedwe ka mikanda [rosary]. Kuchokera ku mulungu wa Dzuwa, [Mai], anatengerako kuyatsa makandulo. Anaonjezeranso chikunja chakupembedza "oyera mtima" akale ndi kukweza "chizindikilo cha mtanda."

Pamene m'episikopi wa Romu ("papa") anayamba kukhala wamphamu ndi chuma zochuruka naphatikiza chipembedzo ndi ndale, anthu okonda Mulungu anazunzidwa. Kwa zaka zambiri, akhristu olungama anathawathawa ndi kubisala m'maenje kuopa kuphedwa. Anapembedza, kufa ndi kuikidwa ndi abwenzi ao m'man-



da okumbidwa m'maenjemo. Akadati andandalikidwe m'mzera woongoka, maenjewo akanaposa mtunda wotalika zipumulo [miles] mazana asanu.

Kuonjezera pothawira pansi pa dziko ndi ku maiko akutali, iwo anachita chisankho chowawa: kupitiriza kukhulupirira Khristu kapena kulora chikunja chosalekanitsa chipembedzo ndi ulamuliro wa dziko. Ambiri anasankha mbali yachiwiriyi.

### *KU ULEMELERO WA MITHRA*

M'chaka cha A.D. 286, asilikari a Gulu la Theban anakana kupereka nsembe ku milungu ya chi-Roma komanso kulonjeza kupha akhristu. Maximillan anakwiya nalamulira kuti aliyense wachikhumi wa asilikariwo aphedwe ndi lupanga. Komabe otsala a asilikariwo sanagonjere mfumuyo. Gulu lina la wachikhumi linaphedwanso. Kenaka, omwe anakhala moyo, analembera kalata mfumuyo, kuti iwo apitirizabe kuopa ndi kulemekeza Mulungu posazunza ndi kupha atumiki ake. Mu mkwiyo wa ngati kuyaka-kutentha kwa ng'anjo mumphamvu yake, Maximillan analamulira kuti asilikari okana kuchita chifuniro chakewo aphedwe. Kutero sikunagwedezebe chikhulupiriro cha amuna pafupifupi 7,000 – omwe ndi m'modzi yemwe sanabwerere m'mbuyo m'chikhulupiriro chao pa Khristu.

M'nthawi yokhayokhayo, osalephera asilikari a mbali zina za chi-Roma anagonjera natumikira milungu ya mafanoyo. Iwo anagwadira Mithra – mulungu wa Dzuwa. Mchitidwe womwe unapangitsa kusintha ndi kubwerera m'mbuyo m'chikhristu.

Nanga Sabata la m'Baibulo la tsiku lachisanu ndi chiwiri, linasinthidwa bwanji kukhala pa Sunday tsiku loyamba la mulungu? Ndi Aroma analisintha:

Kuyambira pachilengedwe, mulungu uli ndi masiku asanu ndi awiri. Atalenga dziko m'masiku asanu ndi limodzi, Mulungu anapumula la chisanu ndi chiwiri, nalipatula likhale lompembedzera lye (Genesis 2:1-3), ndipo mulungu wa masiku asanu ndi awiri ulipobe kufikira lero. Zolembera za mbiri ya dziko ndi za akatswiri a zakayendedwe ka za m'thambo lakumwamba, zikutsimikizira kuti kayendedwe ka masiku a pa mulungu sikanasinthe: mulungu wa masiku asanu ndi awiri uli monga unali pachilengedwe.

Genesis mpaka Chibvumbulutso, mwalembedwa za Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri. Mulibe za tsiku Sunday kuti ndi lopembedza. Nanga tsiku loyambali linadza bwanji?

Kuchokera kunja kwa Baibulo – m'zolembera za mbiri yadziko tipeza yankho. Tipezamo magwero a dzina "Sunday" ndi chiyero cha tsiku'li kuti nzochokera kuchikunja. M'Bukhu Lopatulika, masiku a pa mulungu amadziwika kuti: tsiku loyamba, lachiwiri, kupita chitsogolo. Tsiku lachisanu ndi chiwiri, limatchedwa la Sabata.

M'nthawi ya Khristu, achikunja anayamba kutchula liri lonse la masikuwa ndi dzina lake: Tsiku la Dzuwa, Tsiku la Mwezi ndi ena otere, polemekeza milungu ya zolengedwa za m'mthambo lakumwamba. Gawo ili la chipembedzo chachikunja'li linatchedwa "mulungu wa zam'thambo lakumwamba." Tsiku liri lonse linapatsidwa dzina la mulungu wolilamulira wosiyana ndi milungu ina, wamkuru wa milungu yonseyo analamulira tsiku loyamba la mulungu – natchedwa "Ambuye, Dzuwa." Tsiku lake linatchedwanso – Tsiku la Ambuye Dzuwa.

Awa anali machenjerero a Satana, ofuna kusokoneza Tsiku la Ambuye leni'lo. Sabata la m'Baibulo ndilo Tsiku la Ambuye (Ek. 16:23, 25; 31:15; 32:2), tsiku la Mulungu (Ek. 20:10; Lev. 23:3; Deut. 5:14), tsiku lakelake (Yes. 58:13). Yesu ndi Mlengi wa Sabata ndi zinthu zonse (Aef. 3:9; Yoh. 1:3; Akol. 1:16; Aheb. 1:2; Gen. 2:1-3), ndipo za Umwini tsiku'li anati, "Mwana wa munthu ali mwini tsiku la Sabata" (Mat. 12:8; Mk 2:28). – M'Baibulo tsiku lokhalo la Ambuye ndi la Sabata!

Ngakhale maina a masiku a mulungu ali a tsopano, chipembedzo cha Dzuwa nchakale. Chakhala chiriko kwa zaka zochuruka. "Chipembedzo cha dzuwa ndi choyambirira cha zipembedzo zonse za mafano." – Fausset, Bible Dictionary, p. 666.

Anthu aku Arabia akhala akupembedza dzuwa ndi kayendedwe kake posaliyerekeza ndi kena kapena chizindikilo chiri chonse (Yobu 31:26-27). Abrahamu anatumizidwa ku dziko la lonjezano kumpewetsa chipembedzochi. Aigupto anamutcha mulungu wa Dzuwa'yu Ra, Ono (Heliopolis: Mzinda wa Dzuwa) unali likuru la chipembedzochi. (werengani Yeremiya 43:13).

Polowa m'Kanani pansi pa Yoswa, Ahebri anapeza chipembedzo cha mulungu wa Dzuwa: Baala, wa Fonike; Moleki/Milokomu, wa Ammoni; ndi Hadadi, wa Syria; - yemwenso anatchedwa Mithrasi (Mithra) wa Aperezi – maina onsewa ndi a mulungu wachikunja



wa Dzuwa. Shemishi anali mulungu wa Dzuwa wotchuka ku Maiko aKum'mawa. M'Aigupto munali Aton mulungu wa kayendedwe Kadzuwa. Kachisi wotchuka wa Baalabeki, anapatulikira ku chipembedzo cha Dzuwa.

Chipembedzo cha Dzuwa chakhala chikulimbana ndi chipembedzo cha Mulungu, Mlengi. Pophatikana ndi anthu achipembedzo cha Dzuwa, nthawi zina a Israyeli anagwa mu msampha wakupembedza Dzuwa (Lev. 26:30; Isa 17:8). Mfumu Manase anapembedza Dzuwa (2 Maf. 21:3, 5). Yosiya anaononga magareta ndi zonse zopatulikira ku mulungu wa Dzuwa, napha akavalo onse a mdipiti wa Dzuwa'lo (2 Maf. 23:5, 11-12). Lubano linafukitsidwa pa maguwa a mulungu wa Dzuwa ndi pa matsindwi a nyumba zaolipembedza (Zef. 1:5). Mneneri Ezekieli, anaonetsedwa tchimo lonyansitsitsa la a Israyeli – akupembedza dzuwa mosabisa pakhomo la chipata cholowera ku Kachisi wa Mulungu woona. Anthuwo anayang'ana koturukira dzuwa (Ezekieli 8:16-17). Mu nthawi yathu ino, tikupembedza dzuwa pophatikiza machitidwe a chikhristu ndi a chipembedzo cha Dzuwacho. Zipata zolowera m'nyumba zopempherera ku Ulaya zimakhala kumadzulo. Potsatira miyambo yobwerekera kuchikunjayi opembedza amayang'ana poturukira dzuwa chizindikilo cholemekeza dzuwa'lo m'malo mwa Mulungu. (Zipata za nyumba zopempherera zakale ku Israyeli zimakhala kum'mawa, kuti opembedza aziloza misana yao koturukira dzuwa.)

Patangotsala nthawi yochepa kuti Khrsistu abadwe, masiku a pa mulungu anapatulikira ku milungu yachikunja ya za m'thambo lakumwamba. Tsiku loyamba linali lopembedza dzuwa: nilitchedwa "dies Solis" – tsiku la Dzuwa. Lotsatira lake linatchedwa ("dies Lunae,") – tsiku la mwezi, ndi maina ena.

Zonsezi zinatsutsana ndi chipembedzo cha Bukhu Lopatulika – chomwe chikulimbikitsa kupembedza Mulungu Mlengi wa Zinthu zonse pa tsiku lachisanu ndi chiwiri la pa mulungu, monga mwa Malamulo Khumi. Lamulo lachinai limati: "Uzikumbukira tsiku la Sabata, likhale lopatulika. Masiku asanu ndi limodzi uzigwira, ndi kumariza ntchito zako zonse; koma tsiku lachisanu ndi chiwiri ndilo Sabata la Yehova Mulungu wako; usagwire ntchito iri yonse, kapena iwe wekha, kapena mwana wako wamwamuna, kapena mwana wako wamkazi, kapena wantchito wako wamwamuna, kapena wantchito wako wamkazi, kapena nyama zako, kapena mlendo amene ali m'mudzi mwako; chifukwa masiku asanu ndi limodzi Yehova adamariza zakumwamba ndi zapansi, ndi nyanja, ndi zinthu zonse ziri m'menemo, napumula tsiku lachsanu ndi chiwiri; chifukwa chake Yehova anadalitsa tsiku la Sabata kuti likhale lopatulika." – Eksodo 20:8-11.

La Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri, lomwenso ndi lachikumbutso cha chilengedwe m'Baibulo, ndi lokhalo lakupumula mulungu uli wonse. Tsiku loyamba la mulungu lotchedwa "Tsiku la Dzuwa" ndi lopatulika lakupembedza mulungu wa Dzuwa.

M'nthawi ya Khristu ndi ya atumwi, chipembedzo chobvomerezedwa ndi ufumu wa Aroma'chi chinalibe tsiku lopatulika, koma m'kupita kwa nthawi anthu ambiri m'ufumuwo anayamba kusunga Sunday. Iwo anatero potsanzira chikoka cha asiikari a chi-Roma omwe ponka akumenya nkhonda ndi kusungitsa mtendere m'maiko akutali, anabwera ndi miyambo komanso zipembedzo za tsopano. Chipembedzo chotchuka cha zonsezo chinali cha Mithraim.

Mithra amapembedzedwa monga mulungu wopatsa mphamvu ndi wa nkhondo. M'zaka za zana loyamba A.D., Mithraim anatengedwa kukhala mulungu wa Dzuwa woposa milungu ina yonse m'Ufumu wa Aroma. Aroma nampatsa mulungu wachikunjayu dzina – Sol Invitus, kutanthauza " Dzuwa Wosaoneka." Iye anakondedwa ndi asilikari a chi-Roma, kenaka anthu ochurukitsa anayambanso kumpembedza. Pakatikati pa zana lachiwiri la zaka za A.D., chipembedzo cha Mithraim, mulungu wa Dzuwa chinakhala chipembedzo chachikuru, nichipikitsana ndi Chikhristu.

Ili linali chenjerero lakuya la Satana loyesetsa losokonezera anthu kuti asapembedze Mulungu woona. Chipembedzo cha Mithraim chayesetsa kutsanzira chipembedzo cha Khristu m'njira zingapo: chiri ndi mulungu-mpulumutsi amene anafa, nauka kwa akufa, kubadwa ndi kuuka kwa mulungu-mpulumutsiyo kumakumbukidwa pa Dec. 25 chaka chiri chonse. Chiri ndi migonero [misa] momwe okhulupirira amalumikizana ndi Mithrayo. Olowa m'chipembedzochi, amabatizidwa (poima kunsi kwa chitsulo chofira ndi moto pomwe pamagonekedwa ng'ombe yophedwa yamphongo). Chiri ndi tsiku limodzi lopatulikira Mithrayo – loyamba la mulungu – Tsiku la Dzuwa. Chatsanzira zambiri za kapembedzedwe koona kuposa zonse za chikunja.

Pang'ono pang'ono tsiku latsopano lakupumula la chi-Roma'li linachuka, anthu achikunja analisunga Sunday kukhala lopatulika, monga njira yolemekezera Mithra. Mulungu wachikunjayu anapembedzedwa ndi asilikari a chi-Roma; chifukwa mkapembedzedwe kake mumachitika masewera a luso lolimbitsa thupi komanso ofanana ndi maphunziro a nkhondo.

Atsogoleri ankhondo ndiwo kawirikawiri amalowa ufumu , Akaisara olamulira akamwalira. Kutero kunathandiza chi-Mithra kufalikira mosabvuta m'Romu. Ngati moto pauzdu wouma chinafalikira m'madera onse a ufumu wa Aroma.

Kulowa kwa atsogoleri a nkhondo, Akaisara akafa, kunapatsa mwai Constantine – yemwe banja lake linkapembedza Dzuwa – kukhala mfumu – ndipo mogwirizana ndi atsogoleri a Mpingo wa Chikhristu, ku Romu, analilowetsa tsiku [Sunday] lopatulikira Mithra m'chipembedzo cha Mulungu Wakumwamba.

M'katikati mwa zaka zana lachiwiri A.D., ziphunzitso za chi-Mithra zinakhazikika mwa aphunzitsi a Sukulu ya Ukachenjede ya Mau a Mulungu m'Alexandria. Iwo anaphunzitsa maganizo ndi machitidwe achikunja kwa ophunzira ao. Chikoka chochokera ku Alexandira'chi chinathandizira atsogoleri a Mpingo wa Chikhristu ("apapa"), m'Romu, kutengerako ziphunzitsozo ndi miyambo za chikunjazo, pozitcha "kuwala kwa tsopano." Posakhalitsa, ulamuliro wa Aroma unakhazikitsa lamulo lokakamiza Mpingo wa Chikhristu kugonjera zolakwikazo.

Mbiri ikuti ansembe a Kachisi wa Dzuwa, ku Romu, amatchedwa "aepiskopi [pontiffs]." Anali ansembe a mulungu wao yemwe amafa-nkuuka, mulungu-mpulumutsi Mithra, ndiponso "Achiwiri [Vicegerents]" ( pa ulamuliro kwa iye) mu Mpingo wa chi-Mithra. M'kupita kwa zaka atsogoleri a Mpingo wa Chikhristuwo, anadzitengera maudindo awiriwo podzitchanso "achiwiri" kwa Khristu ndi "aepiskopi" omwe adzigwadiridwa ndi kupatsidwa ulemu ndipo osatero aziphedwa.

M'kati mwa zaka zana lachiwiri, A.D. 150 (zaka 117 pambuyo pa imfa ya Khristu), - akhristu okonda za dziko, m'Alexandria ndi Romu, anayamba kusunga Sunday lopatulika. Zifukwa zosungira tsiku'lo amati limawapangitsa iwo kukhalirana bwino ndi abale omwe anali m'chipembedzo cha chikhunjacho – komanso kuti Chikhristu chilandiridwe ndi achikunjawo. Uku kukungofanana ndi "kulitembenuzira dziko" ku Chikhristu pakuchita chikunja komwe tikukuchita lero.

Chipembedzo cha Mithra chinakhala cha ulamuliro wonse, ndi chotsogola cha zipembedzo zonse, kufikira pamene Constantine I anagonjetsa Licinius m' A.D. 323. Kuyambira pamenepo, Constantine anagwira ntchito limodzi ndi aepisikopi achikhristu a Romu – nakhazikitsa Chikhristu chachikunja cha chi-Roma chomwe chinakhala cha ufumu wonse.

Koma mkupita kwa nthawi, chi-Mithra chinafa – Satana sanafunenso kuchigwiritsa ntchito – chifukwa Romu yense anali mu "Chikhristu Chakugwachi" nutchedwa "Mzinda Watsopano wa Dzuwa."

## *MZINDA WA DZUWA*

Pa March 7, 321 lamulo la mgwirizano linayembekezedwa-nthawi yaitali linakhazikitsidwa – kugwirizanitsa zipembedzo zikuruzikuru ziwirizi kukhala Chipembedzo chimodzi cha Boma. Ili ndi lamulo lotchuka la Constantine la Sunday – tsiku la Dzuwa, lokakamiza kusunga tsiku la Ambuye Mithra, – kukhala lakupembedza la anthu onse m'maiko a m'ufumu wake:

"Oweruza milandu onse ndi anthu a m'mizinda ndi ogwira ntchito za mitundu yosiyanasiyana apumule pa Tsiku lolemekezeka la Dzuwa [Sunday]; pomwe onse okhala m'midzi, mwakufuna kwao ali ndi ufulu wakugwira ntchito zao za m'minda, chifukwa nthawi zina kumapezeka kuti sangachitire mwina pa tsikuli koma kubzala mbeu ndi kulima minda ya mphesa, chifukwa kuti sipangakhalenso tsiku lina lakuchita izi, choncho iwo ayenera kugwira ntchito, osautaya mwai umene waperekedwa kuchokera kumwamba. Lokhazikitsidwa pa lachisanu ndi chinai [Nones] la March, Crispus ndi Constantine pokhala awiriwo oweruza, kwa nthawi ya chiwiri." Zolembedwa m'Code of Justinian, Book III, title 12, law 3.

Constantine sanali m'khristu. Pa nthawi amakhazikitsa lamuloli nkuti akukongoletsa Kachisi wa Dzuwa m'Romu. Constantine anakhazikitsanso lamulo lina lopatsa mphamvu openduza achikunja kuti ndi obvomerezeka mu ufumu wake.

Patadutsa zaka zowerengeka, Constantine anakhazikitsanso malamulo asanu ena olimbikitsa la Sunday la m'A.D. 321.

Tsiku linakhala lalikuru ku timagulu tonse topembedza-Dzuwa, ndi akhristu a akugwa. Limatchedwa "Tsiku lopatuka la Dzuwa." Pamene amakhazikitsa lamulo lokakamiza tsiku'li, nkuti Constantine akupembedza Sol Invictus – "Dzuwa Wosaonekayo" – Ambuye Mithra. Constantineyo anatchedwanso Mkuru wa Aepisikopi [Pontifix Maximus]. Mu limodzi la malamulo ake asanu ndi limodzi a

Sunday'wo, asilikari analamulidwa kuyang'ana dzuwa likamaturuka kum'mawa kwinaku akulankhula mitundu ingapo ya mapemphero a m'mawa a Sunday, monga amachitira onse opembedza Mithra, Serapis, ndi Apolo. Lamulo linati – munthu adzilambira dzuwa likamaturuka." – Victor Duruy, History of Rome, Vol. 7, p. 489.

Constantine analemekeza mulungu wa Dzuwayo, koma mobisalira m'Chikhristu pofuna kugwirizanitsa chikhristu ndi chipembedzo chakecho ndiponso kuti anthu apembedze Mithra ndi kulilemekeza tsiku la Sunday. Mchitidwe wa Usatanawu, unagonjetsa uzimu wa choonadi, nuubala Mpingo wa Aroma wa Chikhristu chakugwa m'zaka zana lachinai A.D.

Izi zinachitika pafupifupi zaka 300 pambuyo pa imfa ya Khristu pa Gologotha, ndiponso pafupifupi zaka 200 pambuyo pakutsirizidwa kwa Bukhu Lopatulika – Sunday linabatizidwa mwachinyengo kukhala la Chikhristu.

Zolembera za mbiri yakale zikutifotokozera kuti Eusbius, episikopi wa Caeserea (c. 260-340), anali bwenzi lokondedwa ndi lokoma m'kamwa la Constantine" (Great Controversy, p. 574). M'zolembera zake, Eusbius akuti mpingo woukira Mulungu'wu ndiwo unamchimwitsa Constantine za lamulo la Sunday. Iye akuti – "Zonse zimene zinali la Sabata, IFE tazisintha kukhala pa Tsiku la Ambuye [Sunday], lomwe ndi lopambana masiku ena onse, lolemekezeka kuposa la Sabata la m'Bukhu Lopatulika." Eusbius, Commentary on Psalms, Psalm 91, in Patrologie Cursus Completus, Series Latina, ed. J.P. Magne, p. 23, 1169-1172.

Ndemanga za akatswiri a mbiri yakale pa umodzi wa chikhristu ndi chikunja cha Maiko odzuka a Kumadzulo:

"Lamuloli linakhazikitsidwa kwa akhristu [ku Romu] kuti alemekezenso zipembedzo zina, kusakanikira nazo ndi kuchitanso miyambo yao kuti achikunjanso achilandire chikhristucho." – Arthur Weigall, (Dr A. E. Weigall [1888-1937].

"Zotsatira zakulimbana [chikhristu ndi chi-Mithra] zikupezeka mu zikondwerero za chikunja zomwe zinabatizidwa m'chikhristu m'zaka zana lachinai zomwe ndi: masiku awiri opatulika a chi-Mithra: a December 25, 'dies natalis solis' [lakubadwa kwa dzuwa] lomwe linabatizidwa kukhala lakubadwa kwa Yesu [Christmas], komanso Sunday, 'lolemekeza Dzuwa,' monga analitchulira Constantine m'lamulo lomwe analikhazikitsa m'321," kulowa m'malo mwa la Sabata. – Walter Woodburn Hyde, Paganism to Christianity in the Roman Empire, p. 60.

(Hyde [1870-?] anali mphunzitsi ndi mlembi wa mbiri yakale wa chi-America).

"Lamulo la chikunja, linakhala la chikhristu; ndipo pokakamizidwa ndi malamulo a dziko, m'zaka za m'zana lachinai, linakhala la mphamvu kufika poletsa kugwira ntchito pa Sunday." –Hutton Webster, Rest Days, 1916, pp. 122-123, 270.

"Pakunena za mphamvu za chipembedzo cha Mithra, tiri ndi umboni kuti si Sabata la m'Bukhu Lopatulika lomwe likusungidwa loyera (lomwe chikhristu chinalitengera ku chi-Yuda, ndipo palibenso lina), koma Sunday lopatulikira mulungu wa Dzuwa Mithra." – H. Lamer, Mithras, Wurterbuch der Antike, 2nd ed., 1933. (Hus Lamer [1873-?] Anali mlembi wofufuza zokwiririka zakale ndiponso wophunzira wa zipembedzo ndi chikhalidwe zachikale).

Ndipo Upapa kudzera mwa Constantine, unautcha mzinda wa Romu, 'Mzinda wa Dzuwa.' Zaka mazana awiri zinachitira umboni wakukhazikitsidwa kwa malamulo oonjezera a Sunday, okakamiza kuti kupembedza Khristu kudzichitika pa tsiku lolemekezera Mithra – ndikuti okana kutero aphedwe.

Chipembedzo cha Mithra, chinafika kumapeto mkati mwa zaka makumi asanu pambuyo pakutha kwa ulamuliro wa Constantine. Chimodzimodzinso cha Isis ndi Horus – Mfumukazi ya Kumwamba wa chi-Aigupto ndi mwana wake wakhanda wamwamuna. Zinatha mkati mwa theka la zaka zana limodzi, ndipo m'malo mwake Aroma anachibatiza ichi m'chikhristu m'chifanizo cha Mariya Woyera, atayangata mwana wa khanda wamwamuna.

Kuchokera pomwe Romu unakhazikitsidwa 'Mzinda wa Dzuwa,' chizunzo cha akhristu chinayamba – chizunzo cha nkhanza chachikuru choposa zomwe zinachitika chisanachitke – chodzidzimutsa. Chinachitika kwa zaka mazana angapo.

Malamulo ena a Sunday oposa khumi ndi asanu anakhazikitsidwa ndi ulamuliro wa upapa wa Mpingo wa Katolika kwa zaka mazana ochuruka zotsatira. Malamulowa anafotokoza zoyenera kuchitidwa ndi kusachitidwa pa Sunday, komanso analetseratu kusunga Sabata. Lamulo liri lonse limanka likukhwima ndikutsatidwa ndi chilango chokhwima. Koma, akhristu olungama anasungabe Sabata la m'Bukhu Lopatulika – ndi kumpembedza Mulungu pa tsiku lachisanu ndi chiwiri la mulungu'li. Kukana kusunga Sunday kunaphetsa chiwerengero chachikuru cha akhristu m'mibadwo yotsatira. Akhristu anazunzidwa ndikuphedwa chifukwa chopembedza Mulungu pa Sabata la m'Bukhu Lopatulika. Koma iwo sanapeputsa chikhulupiriro chao. La Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri liri ndi umboni m'Bukhu Lopatulika; koma chiyero cha Sunday mulibe. Akhristu olungama anachifera choonadi cha m'Bukhu Lopatulika. Iwo anasungabe Sabata loyera'li kufikira mkatikati mwa zaka zana lachisanu. Sozomen ndi Socrates Scholasticus anali akatswiri awiri a mbiri yakale anakhalawo moyo kufikira m'zaka za zana lachisanu A.D. Iwo akuti akhristu ochurukitsitsa (kupatula a ku Romu ndi Alexandria) anapembedzabe Mulungu pa Sabata la m'Bukhu Lopatulika (owerengeka anayamba kusunga Sunday pofuna kukondweretsa atsogoleri a mpingo wa Aroma).

"Ngakhale pafupifupi mipingo yonse padziko lapansi amakondwerera za chiyero cha chinsinsi cha Mulungu la Sabata mulungu uli wonse, koma akhristu aku Alexandira ndi ku Romu, posankha kusunga ina ya miyambo yachikalekale, asiya kusunga Sabata loona." – Socrates, Ecclesiastical History, Book 5, chap. 22.

"Akhristu a ku Constantinople, ndiponso pafupifupi a dziko lapansi lonse, amasonkhana pamodzi la Sabata, ndi pa tsiku loyamba la pa mulungu, chinthu chomwe sichimachitidwa ku Romu kapena ku Alexandria." – Sozomen, Ecclesiastical History, vii, 19, zopezeka m'Select Library of Nicene and Post-Nicene Fathers, 2nd series, Vol. II, p. 390.

Munthu asakunamizeni kuti Khristu ndi atumwi anasunga Sunday, m'zaka za zana loyamba kapena lachiwiri Bukhu Lopatulika litatsirizidwa kulembedwa. Sichinachitike. Chiwerengero chachikuru cha akhristu m'nthawiyi anasungabe la Sabata lachisanu ndi chiwiri kukhala lopatulika la Mulungu – kufikira m'zaka zana lachisanu (A.D. 400-499). Ndi pakuzunza ndi kukhetsa mwazi unasefukira m'miseu ya m'mzindamo ngati mitsinje ya madzi, pomwe mpingo wopandukira Mulungu wa Aroma, unagonjetsa numpanga Romu 'Mzinda wa Dzuwa' kudzera mu ulamuliro wake wochokera kwa 'Mulungu wa Dzuwa.'

Yesu analosera m'mbuyomo za chizunzochi – kuti chidzachitika.

## ULOSI NDI PEMPHERO ZOIWALIKA

Ndipo ophunzira ake, anamfotokozera Iye za mamangidwe a Kachisi. Josephus, mlembi wa Chiyuda, akuti Kachisi anamangidwa pa maziko a miyala ikuruikuru yotalika mapazi makumi anai mphambu awiri m'litali uli wonse.

Atatha, ophunzirawo anakhala chete nagwidwa mantha akuru pa zomwe Iye anawayankha, "Simuona izi zonse kodi? indetu ndinena kwa inu, Sipadzakhala pano mwala umodzi pa unzake, umene sudzagwetsedwa." Mateyu 24:2.

Pogwidwa ndi mantha, ophunzira anamfunsa Khristu awauze tsiku lomwe zimene Iye analankhula zidzachitika – komanso zina zosonyeza kuyandikitsa kwa nthawi yachimaliziro. "Mutiuze ife zija zidzaoneka liti? Ndipo chizindikilo cha kufika kwanu nchiyani, ndi cha mathedwe a nthawi ya pansi pano?" Mateyu 24:3.

Yankho la Yesu linadzadza mutu 24 wa Mateyu. Mu yankholo muli malangizo – machenjezo a mpamhvu. Muli chidziwitso chofunika kwa tonse tikuyang'anizana ndi zirinkudzazo. Chothandiza ku miyoyo yofunitsitsa kupanga ubale – wotsimikizika ndi Yesu m'nthawi yakuyesedwa irikudza'yi.

M'ndime 15 mpaka 20, Yesu anafotokoza choyenera kuchita zizunzo zikamatigwera; - tizithawa. Anatinso tizipemphera kosalekeza mogwirizana ndi malamulo a Mulungu – kufikira Iye adzabweranso: "Ndipo pempherani kuti kuthawa kwanu kusakhale pa nyengo yachisanu, kapena pa tsiku la Sabata." Mateyu 24:20.

M'ndime 21 ndi 22, Iye akutilangiza kuti padzakhala masauko akuru, koma tidzapulumukamo.

Pamene anali pansi pano, Yesu anatipatsa chitsanzo chakumvera ndi kuchita Malamulo Khumi a Mulungu. Nati, "Musaganize kuti ndinadza Ine kudzapasula chilamulo kapena aneneri: sindinadza kupasula, koma kukwaniritsa. Pakuti indetu ndinena kwa inu, Kufikira litapitirira thambo ndi dziko, kalemba kakang'ono kamodzi kapena kansonga kake kamodzi sikadzachokera kuchilamulo." Mateyu 5:17-18.

"Chifukwa chake yense wakumasula limodzi la malangizo amenewa ang'onong'ono, nadzaphunzitsa anthu chomwecho, adzatchulidwa wamng'onong'ono mu Ufumu wa Kumwamba; koma yense wakuchita ndi kuphunzitsa awa, iyeyu adzatchulidwa wamkuru mu Ufumu wa Kumwamba." – Mateyu 5:19.

Ataphunzitsa iwo za kufunika kwa moyo wa umulungu, anaphedwa naikidwa m'manda. Ali chigonere m'manda, ophunzira ake anasunga Sabata la m'Baibulo – popumula, nabweranso kudzagwira ntchito yolidzoza thupi lake, tsiku loyamba – la mulungu [Sunday] chifukwa sanathe kutero pa Friday. (Luka 23:50-24:4; Mateyu 27:55-28:2; Marko 15:42-16:9).

Ophunzira anapitiriza kulisunga Sabata m'mautumiki ao onse (Machitidwe 13:14-16, 40-46; 16:12-15; 17:1-4). Nati iwo ayenera kumvera Mulungu kuposa munthu (Machitidwe 5:29), Paulo anadzifunsa ndi okhulupirira tonsefe: "Potero kodi lamulo tiyesa chabe mwachikhulupiriro? Musatero ai; koma [ndi chikhulupiriro] tikhazikitsa lamulo." Aroma 3:31.

M'mautumiki ao, anthu olungama amapemphera monga Yesu anawaphunzitsira. Anapempha Mulungu awathandize ndi kuwapatsa mphamvu ya kulisunga Sabata ngakhale azunzidwe ndi kuphedwa. Pemphero lao limayankhidwa.

Mosakhalitsa chinadza chizunzo chachikuru – chizunzo chochititsa mantha chimene Yesu analosera ndi kuchenjeza kuti chinalinkudza – chizunzo cha kuphasulidwa kwa mzinda wa Yerusalemu ndi

Kachisi anali momwemo.

Zaka makumi atatu ndi zisanu kuchokera pomwe chinaloseredwa, chizunzocho ngati namondwe chinadza mwadzidzidzi, m'phwasulo losalimvetsetsa munthu. M'mapiri a Samariya ndi m'miseu ya Galileya, momwe Yesu anayendayendamo ndi kulankhula ndi ophunzira ake, anthu zikwizikwi anaphedwa ndi lupanga komanso akasidi a nkhondo. Umodzi umodzi wa mizinda yodalirika ya Ayuda inasaladzidwa nikhala milu ya miyala ndi mabwinja. Nyanja imene Yesu anailamulira kukhala bata itabvunduka ndi namondwe, inafiira ndi mwazi wa anthu m'nthawi ya nkhondo ya Taricheaeyi, . Pamene izi zinali kuchitika, anthu a Mulungu anapemphera kosalekeza pemphero lomwe Yesu anatiphunzitsa.

Chiyambi cha nthawi yachimaliziroyi chinafika pa Yerusalemu m'August, 66 A.D. Kwa zaka zinai zakutsogolo Yerusalemu sanauone mtendere pakuti Myuda anamenyana ndi Myuda mnzake kapena Myuda kumenyana ndi Mroma, mkati kapena kunja kwa malinga a mzindawo. Pakuchitika izi akhristu sanasiye kupemphera monga Yesu anawalangizira.

Gulu lina la asilikari a chi-Roma linapanikizidwa m'Yerusalemu ndikukanthidwa molapitsa, ichi chinadzutsa mkwiyo wa Cestius Gallus, mkuru wa gulu lankhondo la chi-Roma ku Syria yemwe anachita chandamale kulowera chakumwera komwe kunali gulu lina la asilikari 30,000. Kumeneko Iye anaphwasula ndi kuotcha mzinda wa Yopa ndikulanda Galileya ndi madera a mbali ya nyanja, natembenuka kulozanso ku Yerusalemu. Mtopola utakura, asilikari a Chiyuda omwe anaikidwa m'kati mwa malinga kuutchinjiriza anatsala pang'ono kuupereka kwa mdaniyo, - koma chozizwa chinachitika: mofulumira Cestius anangobwebvuka osalowa m'mzindamo. Kutero kunalimbikitsa mtima ankhondo a Chiyuda, kuthamangitsa ndikukantha ankhondo a chi-Romawo kufikira pakugwa pa mdima womwe unapulumutsa Aroma kuti asatheretu. Ayuda analanda akasidi ankhondo a Cestius ndi kupha asirikali 5,300 oyenda pansi, ndi 380 a pa akavalo. Ayuda anabwerera m'Yerusalemu, mokondwera osalingirira za choopsya chinati chiwagwere zisanathe zaka zitatu.

Yesu anauza ophunzira kuti adzazindikira nthawi yomwe adzaturuke mu mzindamo:

"Ndipo pempherani kuti kuthawa kwanu kusakhale pa nyengo yachisanu, kapena pa tsiku la Sabata." Mateyu 24:20.

Ulosiwu unakwanitsidwa.Pokumbukira zomwe anauzidwa zaka makumi atatu, zisanu ndi chimodzi ndi theka zapitazo, ana a Mulungu anapempheradi kuti awathandize kuti aturuke mu mzindawo – koma pasakhale pa tsiku lopatulika la Sabata.

Atangobwebvuka Cestius, Ayuda natangwanika kumthamangitsa, - ophunzira anazindikira kuti inali nthawi yao yothawa. Dziko lonse ndi m'midzi munali bata; nkhondo inali chakumpoto kwa Yerusalemu. Mosazengereza, wophunzira ali yense anaturuka m'Yudeya kuthawira ku Pella m'dziko la Perea, kum'mawa kwa Mtsinje wa Yordano. Kuthawako sikunachitikedi la Sabata, komanso kunali kwa mtendere. Palibe wophunzira ndi m'modzi yemwe anaphedwa. Mulungu anayankha pemphero lao. Zinachitika izi mwezi wa October m'A.D. 67, m'chaka cha khumi ndi ziwiri cha ulamuliro wa Nero.

M'August, A.D. 70, mzinda wa Yerusalemu unaphwasulidwa chifukwa anthu osankhidwa a Mulungu anampandukira Iye posamvera Mau ndi kusachita Malamulo Khumi. Yerusalemu ndi Kachisi anali momwemo anaonongedwa, pafupifupi zaka makumi anai kuchokera pomwe Khristu analosera.

Pemphero anatiphunzitsa Yesulo silinapherezere. Tikukhala m'nthawi zowawitsa za dziko lapansi; tsiku liri lonse likumadza ndi zobetchera zake. Tisaleme kupemphera pemphero'li – ngati tikufunitsitsa kulisunga Sabata lake – la m'Baibulo – la tsiku lachisanu ndi chiwiri la mulungu m'masautso alinkudza. M'zolembera za mbiri yakale ndi za akatswiri a za m'thambo lakumwamba, tikuzindikira kuti kayendedwe ka masiku a mulungu sikanasinthe ndipo kadzakhalabe ku mibadwo mibadwo. Tsiku lachisanu ndi chiwiri la lero – ndi la Sabata la m'Baibulo lomwe anasunganso Yesu zaka 2,000 zapitazo.

Pemphero'li ndi lathu ngakhale timaliwara. Mpingo wa Aroma, ukuyesetsa kuthetseratu za kusunga Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri. Koma Mulungu sasintha, choncho la Sabata lake silingasinthe. M'Genesis 2:1-3, atangotsiriza kulenga dziko, Mulungu anapereka Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri kwa munthu. Tiyenera kusunga ndi kulilemekeza monga njira yoyamikira mphamvu ya Mulungu yakulenga. M'Eksodo 20:8-11 lamuloli n'lachinai la Malamulo Khumi.

Palibe m'Malemba pomwe Mulungu wasinthapo za chiyero cha Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri ndi kuchiika pa Sunday, tsiku loyamba. Tisadzinamize kuti tikumvera ndi kulemekeza Mulungu posunga tsiku losiyana ndi limene Iye analiika.

Ngati tinaliyiwalapo pemphero'li lomwe Yesu anatiphunzitsa pa Mateyu 24:20, pano tiyeni tichite nalo mosatopa. Chipulumutso cha moyo wathu chidalira pa ili.

Zingatheke kuti – pompano – tiyambe kuchita nalo pempheroli? Za pemphero'li ndi chenjzo lake Yesu Baibulo likuti:

"Ndipo pamene Iye analikukhala pansi pa phiri la Azitona, ophunzira anadza kwa Iye pa yekha, nanena, Mutiuze ife zija zidzaoneka liti? Ndipo chizindikilo cha kufika kwanu nchiyani, ndi cha mathedwe a nthawi ya pansi pano?

"Ndipo Yesu anayankha nati kwa iwo, Yang'anirani, asasokeretse inu munthu. Pakuti ambiri adzafika m'dzina langa, nadzanena, Ine ndine Khristu, nadzasokeretsa anthu ambiri. Koma inu mudzayamba kumva za nkhondo… Pakuti mtundu umodzi wa anthu udzaukirana ndi mtundu wina, ndi ufumu ndi ufumu wina; ndipo kudzakhala njala ndi zibvomezi m'malo akuti akuti [osiyana siyana]. Koma ndizo zonsezi zowawa zoyamba.

"Pomwepo adzakuperekani kunsautso, nadzakuphani; ndipo anthu a mitundu yonse adzadana nanu, chifukwa cha dzina langa. Ndipo pomwepo ambiri adzakhumudwa, nadzaperekana wina ndi mnzake, nadzadana wina ndi mnzake. Ndipo aneneri onama ambiri adzauka, nadzasokeretsa anthu ambiri. Ndipo chifukwa cha kuchuruka kwa kusayeruzika, chikondano cha anthu aunyinji chidzazirala. Koma iye wakulimba chilimbikire kufikira chimariziro, yemweyo adzapulumuka. Ndipo uthenga uwu wabwino wa Ufumu udzalalikidwa pa dziko lonse lapansi, ukhale mboni kwa anthu a mitundu yonse; ndipo pomwepo chidzafika chimaliziro….

"Ndipo pempherani kuti kuthawa kwanu kusakhale pa nyego yachisanu, kapena pa tsiku la Sabata; pakuti pomwepo padzakhala masautso akuru, monga sipadakhale otero kuyambira chiyambi cha dziko, kufikira tsopano, inde ndipo sipadzakhalanso. Ndipo akadaleka kufupikitsidwa masiku awo, sakadapulumuka munthu ali yense: koma chifukwa cha osankhidwawo masiku awo adzafupikitsidwa…

"Ndipo pomwepo padzaoneka m'thambo chizindikilo cha Mwana wamunthu alinkudza pamitambo yakumwamba, ndi mphamvu ndi ulemelero waukuru. Ndipo Iye adzatumiza angelo ake ndi kulira kwakukuru kwa lipenga, ndipo iwo adzasonkhanitsa osankhidwa ake kumphepo zinai, kuyambira malekezero a thambo kufikira malekezero ake ena." Mat. 24:1-31.

Apa zikumveka bwino kuti Yesu amalosera za zochitika za mtsogolo mpaka pa tsiku la Kudza kwake Kwachiwiri. Tinayenera kusunga Sabata m'mibadwo yathu yonse kufikira lero.

Anthu ambiri ndi okhumudwa chifukwa cha a mipingo ya Mpanduko yomwe akupitirizabe kusunga tsiku loyamba [Sunday] la pa mulungu kukhala lopatulika. Chifukwa chimene iwo asokonekerera nacho ndi chakuti Consatntine, mogwirizana ndi atsogoleri a mpingo wa Romu, anayesetsa kusintha Sabata kuliika pa Sunday m' A.D. 321. Ichi chinachitika – zaka 290 imfa ya Khristu itachitika pa Gologotha, ndiponso zaka 226 bukhu lotsirizira la m'Baibulo litalembedwa.

Mulibe za kupatulika ndi chiyero cha Sunday – m'Baibulo. Sizoonanso kuti Sabata linasinthidwa kupita ku Sunday chifukwa timawerenga kuti atumwi ananyema mkate pa Sundaylo ndiye kuti amalisunga. Komanso sizoona kuti tizisunga Sunday m'malo mwa Sabata la m'Baibulo "pofuna kulemekeza kuuka kwa Yesu komwe kunachitka pa tsiku'li." Choonadi cheni cheni ndi chakuti tiyenera kusunga Sabata chifukwa Mulungu anatilamulira kutero m'Mau ake – osati pongoganiza mwa miyambo ndi umunthu..

## KULENGEDWA KWA DZIKO

Mulungu analenga dziko'li m'masiku eni eni asanu ndi limodzi, napereka Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri kwa munthu. Iye nafuna tidzikumbukira kuti ali Mlengi chifukwa kungomuiwala kungapangitse dzikoli losakoma kukhalamo.

Chifukwa ninji nkofunika tidzimkumbukira Mlengi wathu? Iye, yekhayo, ndi Mlengi ayenera kupembedzedwa. Tiyenera kumgwadira ndi kumkonda kuchokera pansi pa mtima. Onse onyalanyaza Sabata mwadara koma akuzindikira amatayika mu uzimu. Kupembedza Mulungu kumakhala kwa tanthauzo ngati Sabata likusungidwa.

Pa Tsiku Lachisanu ndi Chimodzi la mulungu Wakulenga, Mulungu anapanga nyama za pa mtunda ndi munthu. Pa tsiku lachisanu ndi chiwiri Iye anapumula kutipatsa chitsanzo. Ndipo anadalitsa tsiku'li pa mulungu woyambawo – polipatula ndi kuliyeretsa, ndi kuti mtundu wa anthu upitirize kulisunga m'nthawi zonse.

"Mulungu ndipo anadalitsa tsiku lachisanu ndi chiwiri, naliyeretsa limenelo: chifukwa limenelo adapuma ku ntchito yake yonse imene Mulungu anailenga ndi kupanga." – Gen. 2:1-3.

Tsiku la Sabata ndi lake la Mulungu – Tsiku la Ambuye – lopatsidwa kwa munthu adzipembedzeramo.

Yesu Khristu ndiye analenga zinthu zonse (Akol. 1:16; Yoh. 1:3; Aheb. 1:1-3). Iye akudzifotokoza kuti ndi Ambuye wa Sabata (Mat. 12:8; Mk 2:28). Tsikuli ndi la Ambuyedi. Akulitcha "Tsiku langa lopatulika" m' Yesaya 58:13. Ndichomwe mtumwi Yohane ankatanthauza m'Chibvumbulutso politchanso, "Tsiku la Ambuye" (Chibv. 1:10).

Khristu samangofuna kuti tizisunga Sabata mwa ife tokha, - koma tiliphunzitsenso kwa anthu otizungulira omwe mwina analiwala kapena sakulidziwa kuti lilembedwenso m'miyoyo yao ndi kusungidwa m'mitima mwao.

"Ndipo iwo amene adzakhala a iwe adzamanga malo akale abwinja; udzautsa maziko a mibadwo yambiri; udzatchedwa Wokonza pogumuka, Wakukwezera njira

zakukhalamo. Ukaletsa phazi lako pa Sabata, ndi kusiya kuchita kukonndwerera kwako tsiku langa lopatulika, ndikuyesa Sabata tsiku lokondwa…, pomwepo udzakondwa mwa Yehova;… pakuti pakamwa pa Yehova panenapo.” Yesaya 58:12-14.

Yesu analenga Sabata chifukwa cha munthu – mtundu wonse wa anthu – zaka 2,000 Myuda woyamba, Abrahamu asabadwe. “Mwana wa munthu ali mwini dzuwa la Sabata lomwe.” Marko 2:28.

Panadutsa zaka zokwanira 2,500 dziko litalengedwa ndiponso Sabata la m’Baibulo litaperekedwa koyamba ku mtundu wa anthu – pomwe Malamulo Khumi a Mulungu amalembedwa kwa nthawi yoyamba.

Anthu ena amaganiza kuti pachiyambi pachilengedwe kunalibe malamulo kufikira pamene analembedwa pa magome a miyala pa Phiri la Sinai. Kukanakhala kuti kunalibe Malamulo, Kaini sakanenedwa kuti wachimwa pakumpha Abele. Koma Genesis 4 likutitsimikizira kuti kunawerengedwa tchimo kwa Kaini atapha mbale wakeyo kutanthauza kuti lamulo linalipo. Ndi kholo ndani angabereke mwana wake m’dziko lapansi – osamphunzitsa mwanayo malire a kakhalidwe kake? Mwana wosalangizidwayo angakure mopulukira. Atate wathu, Mulungu wa Kumwamba, pokhala kholo labwino anatipatsa malamulo ake kuyambira pachiyambi kuti mtumdu wa anthu usapulukire.

Malamulo analipo chilengedwe chisanakhale: Mulungu atangowalenga Adamu ndi Hava anawapatsa malamulowo. Zaka 2,500 kuchokera pomwe Mulungu anapatsa iwo Sabata, analemba awa pa tanthwe – chinthu cholimba ndi chokhalitsa.

## KUKOMANA NDI MFUMU

Mulungu anaturutsa anthu ake, Israyeli, m’dziko la Aigupto kuti akamtumikire Iye. Anawasankha adziwitse chifuniro chake kwa anthu okhala pa dziko. Iye anadza nao ku chigwa chinali patsoglo pa Phiri la Mose [Jebel Musa] kuti awaonetsere Umulungu wake, kuti auchite, nauphunzitse kwa anthu owazungulira kunthawi zonse – kuti dziko lizindikire choonadi, kuti kupatula milungu ya mafano pali Mulungu woona; yemwe ali ndi Lamulo Lopatsa Moyo - Malamulo Khumi omwe munthu akawachita amakhala nao ndi moyo.

Atafika ku phiri (la Sinai/Horebu), anthuwo anamanga misasa yao m’chigwa kunsi kwa malinga a matanthwe akuru, kuyembekezera bvumbulutso lina la Mulungu pa iwo.

Anadza kukomana ndi Mfumu ya mafumu onse.

“M’mawa wa tsiku lachitatu [kuchokera tsiku anafika ku phirilo], maso a anthuwo anakhala chiyang’anire ku phirilo, lomwe nsonga zake zinakutidwa ndi mtambo wochindikara, womwe unanka ukuderadera, kufikira phiri lonselo linakutidwa mu mdima wandiweyani. Kenaka kunamveka mau ngati a lipenga, kuitana anthuwo akomane ndi Mulungu wao; ndipo Mose anatsogolera iwo ku tsinde la phirilo.

“M’chimdimamo mudaonekera kung’anima ngati kwa mphenzi, ndipo kugunda ngati kwa bingu kunamveka mobwereza bwereza ndi molandizana pakati pa nsonga zazitali za phirilo. ‘Ndipo Phiri la Sinai linapfuka utsi, chifukwa Ambuye anatsika pa ilo m’malawi a moto: ndipo utsi unapfukawo unakwera ngati utsi wa ng’anjo ya moto, ndipo phiri lonse linagwedezeka kwakukuru.’ ‘Ulemelero wa Mulungu unaonekera ngati moto woyaka pamwamba pa phirilo pamaso pa msonkhano wa khamulo. Ndipo ‘liu ngati la lipenga linakwererakwerera’.. Kenaka kugundako kunasiya; ndi liu la kulira kwa lipenga silinamvekenso; dziko linakhala bata. Panakhala mphindi za bata lalikuru ndithu – ndipo m’bata limenelo Mau a Mulungu anamveka.

“Pakulankhula kuchokera mkati mwa mdimawo, alikuima Iye pa phiripo, wozungulidwa ndi makamumakamu a angelo, Mulungu anapereka Lamulo lake.” – Patriarchs and Prophets, 304.

Ndi litinso pambuyo pa chochitika cha pa Phiri la Sinai’chi, m’Chipangano Chakale, pomwe Mulungu anaonetseranso ukuru, mphamvu ndi ulemelero zake ku msonkhano wa anthu? Palibe. Nanga ndi liti m’Chipangano Chatsopano, kufikira mu nthawi yathu ino, pomwe Iye anachita chinthu ngati ichi kapena choposa apo? Pa imfa ya Ambuye Yesu.

Ndi chifukwa chiyani Iye anachichita ichi? – Mulungu anafuna kuti anthu a padziko lapansi – omwe anaona izi zikuchitika, komanso amene kunalibe pakuwerenga, zolembedwa ndi oona ndi maso – azindikire kuti Lamulo Lopatsa Moyo - Malamulo Khumi ndi lofunikira m’miyoyo yao. Ndipo alitenge kukhala chowatsogolera m’zonse azichita.

Choonadi chokhala m’magawo awiri ngati lupanga lakuthwa konsekonse chikuti tingathe, ndipo tiyenera, kumvera Mulungu – ndiponso tingathe ndiponso kuchita chifuniro chake mwa chisomo cha Yesu Khristu – chokhazikika pa maziko Malemba oyera. “Khulupirira ndi kumvera, pakuti palibenso njira ina, yakukondwa mwa Yesu, komatu kukhulupirira ndi kumvera” ndiwo maziko eni eni a chikhristu. Ichi ndicho chikalata chathu cholowera kumwamba. Mulungu sadzalora munthu ali yense kulowa kumwamba, amene, pokhala pansi pano, anasankha kukhala m’uchimo pokana kumvera Malamulo Ake.

Werengani Malamulo a ku nthawi



zonse a Mulungu opatsidwa ku mtundu wa anthu. Awa ali angwiro chifukwa anapatsidwa kwa ife ndi Mlengi wathu:

* * * * * * *

“NDIPO MULUNGU ANANENA MAU ONSE, NATI:

“Ine ndine Yehova Mulungu wako, amene ndinakuturutsa iwe ku dziko la Aigupto, ku nyumba ya akapolo.

1. “Usakhale nayo milungu ina koma Ine ndekha.

2. “Usadzipangire iwe wekha fano losema, kapena chifaniziro chiri chonse cha zinthu za m’thambo la kumwamba, kapena za m’dziko lapansi, kapena za m’madzi a pansi pa dziko; usazipembedzere izo, usazitumikire izo; chifukwa Ine Yehova Mulungu wako ndiri Mulungu wansanje, wakulanga ana chifukwa cha atate ao, kufikira mbadwo wachitatu ndi wachinai wa iwo amene akudana ndi Ine; ndi kuwachitira chifundo anthu zikwizikwi a iwo amene akondana ndi Ine, nasunga malamulo anga.

3. “Usatchule dzina la Yehova Mulungu wako pachabe; chifukwa Yehova sadzamuyesa iye wosachimwa, amene atchula pachabe dzina lakelo.

4. “Uzikumbukira tsiku la Sabata, likhale lopatulika. Masiku asanu ndi limodzi uzigwira, ndi kumariza ntchito zako zonse; koma tsiku lachisanu ndi chiwiri ndilo Sabata la Yehova Mulungu wako; usagwire ntchito iri yonse, kapena iwe wekha, kapena mwana wako wamwamuna, kapena mwana wako wamkazi, kapena wantchito wako wamwamuna, kapena wantchito wako wamkazi, kapena nyama zako, kapena mlendo amene ali m’mudzi mwako; chifukwa masiku asanu ndi limodzi Yehova adamariza zakumwamba ndi zapansi, ndi nyanja, ndi zinthu zonse ziri m’menemo, napumula tsiku lachisanu ndi chiwiri; chifukwa chake Yehova anadalitsa tsiku la Sabata kuti likhale lopatulika.

5. “Uzilemekeza atate wako ndi amako; kuti achuruke masiku ako m’dziko limene Yehova Mulungu wako akupatsa iwe.

6. “Usaphe.

7. “Usachite chigololo.

8. “Usabe.

9. “Usamnamizire mnzako.

10. “Usasirire nyumba yake ya mnzako, usasirire mkazi wake wa mnzako, kapena wantchito wake wamwamuna, kapena wantchito wake wamkazi, kapena ng’ombe yake, kapena buru wake, kapena kanthu kali konse ka mnzako.” – Eksodo 20:1-17.

* * * * * * *

Mulungu analankhula Malamulo Khumi pa Phiri la Sinai, nawalemba pa tanthwe, kukhala Lamulo la Moyo ku mtundu wa anthu. Tanthwe ndi chinthu cholimba, chokhalitsa. Kulembedwa pa tanthwe, kunaimira umyaya wa Malamulo a Mulungu monga anali matanthwe anatchingawo mbali zansonga zazitali za Sinai zinali pamwamba pa anthu omvetsera Malamulowo.

“Malangizo ake…achirikizika ku nthawi za nthawi.” – Mas. 111:7-8.

Malamulo sanangolembedwa pa tanthwe. Komanso kuti akhazikike ndi kusungidwa m’mitima mwathu – powachita!

“Ndipo ndidzaika mzimu wanga m’kati mwanu, ndi kukuyendetsani m’malemba anga; ndipo mudzasunga maweruzo anga ndi kuwachita.” Ezek. 36:27.

“Ndidzaika chilamulo changa m’kati mwao, ndipo m’mitima mwao ndidzachilemba.” Yer. 31:33.

“Pakuti ili ndi pangano ndidzalipangana ndi nyumba ya Israyeli, atapita masiku ajawa, anena Ambuye: Ndidzapatsa malamulo anga kuwalonga m’nzeru zao, ndipo pamtima pao ndidzawalemba iwo; ndipo ndidzawakhalira iwo Mulungu, ndipo iwo adzandikhalira Ine anthu.” Aheb. 8:10.

Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri ndi chizindikilo chakuti Mulungu ndiye Mlengi ndi Mpulumutsi wathu:

“…azisunga Sabata, kuchita Sabata mwa mibadwo yao, likhale pangano losatha [lamyaya]; ndicho chizindikilo chosatha pakati pa Ine ndi ana a Israyeli; pakuti Yehova analenga zam’mwamba ndi dziko lapansi masiku asanu ndi limodzi, napumula tsiku lachisanu ndi chiwiri, naonanso mphamvu.” Eks. 31:16-17.

“Muzisunga masabata anga ndithu; pakuti ndiwo chizindikilo pakati pa Ine ndi inu mwa mibadwo yanu; kuti mudziwe kuti Ine ndine Yehova wakukupatulani.” Eks. 31:13.

“Ndipo ndinawapatsanso masabata anga akhale chizindikilo pakati pa Ine ndi iwo, kuti adziwe kuti Ine ndine Yehova wakuwapatula.” Ezek. 20:12

Muzipatulanso masabata anga, ndipo adzakhala chizindikilo pakati pa Ine ndi inu, kuti mudziwe kuti Ine ndine Yehova Mulungu wanu.” Ezek. 20:20.

Kusunga malamulo a Mulungu ndi la Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri ndi chizindikilo chakuti Mulungu ndi Mlengi wathu (Eks. 31:17), Mpulumutsi wathu (Ezek. 20;12), ndife anthu ake (Ezek. 20:20), ndiye wakutipatula (Eks. 31:13).

Udindo wathu kwa Mulungu uzindikirika kuchokera m'Bukhu Lopatulika. Sipakutengera zomwe anthu otizungulira akuchita. Ndi chinthu chomwe chichokere m'mau a m'Baibulo. Nthano ya mlonda wa chitsamba cha Rose m'munsimu itithandize kumvetsa udindo wathu:

## *KUTSEGULA NKHOKWE YA ZOLEMBEDWA*

"Atsogoleri, kodi munthuyo akulondera chiyani?"

Mtsogoleri anayankha: "Chomwe ndikudziwa ndichakuti malamulo amati pamalopa padzikhala mlonda nthawi zonse."

Panadutsa zaka zana limodzi, ndipo kumapeto kwa zaka khumi ndi zisanu ndi zitatu za zanalo, Katerina, Mfumukazi ya Russia, anadzala chisamba cha maluwa a Rose pamalopo.

Mkupita kwa nthawi chitsambacho chinafa, ndipo palibe munthu wina anaganiza zochotsa lamulo lolondera pamalopo, linakhazikitsidwa ndi mfumukaziyo.

Ndipo kwa zaka zana limodzi anthu anakhala akulondera panadzalidwa chitsambacho – osadziwa chimene amalondera.

Anthu akusunga Sunday. Akupumula pa tsikuli; nkumakhala ndi matumiki akupembedza pa tsikuli mulungu uli wonse. Ambiri amatero poganiza kuti ndi Mulungu analamulira kutero.

Ndi m'Mau a Mulungu momwe tingapeze choonadi za tsiku'li. Mulibe chiyero cha Sunday m'Bukhu Lopatulika. Mulibe umboni uli wonse m'masamba a Bukhu Loyera wakuti Mulungu anasintha la Sabata kuliika pa Sunday.

M'mbiri yakale, tikupeza kuti kusunga Sunday, kuli ngati kulondera chitsamba cha Rose, – tsiku lomwe–linangokhazikitsidwa mu Mpingo wa Chikhristu, osati ndi Mulungu. Koma zaka mazana awiri Baibulo litalembedwa kale, ndiponso mlembi wotsiriza wa Baibulo atafanso kale.

Mulungu alitu ndi cholinga chabwino ndi moyo wathu. Ndipo ali gawo la cholingacho, monga tiri eni akefe. Akutiitana kupumula naye limodzi pa tsiku lake lopatulika; kuti pakutero tizame m'chikhulupiriro mwa Iye. "Wakukhala mwa Ine, ndi Ine mwa iye, ameneyo abala chipatso chambiri; pakuti kopanda Ine simungathe kuchita kanthu." Yohane 15:5.

Sabata ndi mphatso ya mtengo wapatali yopatsidwa mwapadera kwa ife – kuchokera ku Paradiso. Nkofunikira kulisamala. Tizilisunga chifukwa ndi chikumbutso cha magwero a kulengedwa kwa miyoyo yathu.

Mulungu analilenga Sabata kuti likhale nthawi imene Iye ndi ana ake a dziko lapansi adzikhalira limodzi. Chifukwa cha ichi Mulungu analamulira Sabata kukhala "pangano losatha" (Eks. 31:16-17). Anthu ake okhulupirika adzalilemekeza Sabata, kwa myaya, m'dziko latsopano:

"Pakuti monga m'mwamba mwatsopano ndi dziko lapansi latsopano limene ndidzalenga, likhalabe pamaso pa Ine,.. kuyambira Sabata lina kufika kulinzake, anthu onse adzafika kudzapembedza pamaso pa Ine, ati Yehova." Yes. 66:22-23.

Kodi myaya udzatalika bwanji? Kutalika kwa myaya kudzadziwidwa ndi iwo amene adzakhalemo. Sabata liri chimodzi cha zizindikiritso za myayawo. Sabata la m'Bukhu Lopatulika ndi ulalo wolunzanitsa anthu ndi Mulungu. Tichiphunzitse choonadi'chi, ndikuchilandira eni ake'fe. Ndi chokhacho chingatisunthire kwa Mlengi wathu. (Eks. 31:13, 17; Ezek. 20:12, 20). Kusunga Sabata koyenera kumachitika tikakhalanso ndi chikhulupiriro mwa Khristu, anthu onse otero adzalisunga moona mtima. Kupembedza Mulungu pa tsiku'li kumatiika m'chiyero chake m'masiku onse a m'kati mwa mulungu.

Yesu Khristu anabadwa m'dziko lapansi'li patangotsala kanthawi pang'ono kuti Chikhristu chikhazikitsidwe. Anakula ndi kubatizidwa m' A.D. 27, nayamba utumiki wake wa zaka zitatu – ndi – theka.

Ali m'dziko lapansi, Yesu anatipatsa chitsanzo chakumvera ndi kalemekezedwe ka tsiku la Sabata lomwenso analipatsa ku mtundu wa anthu pachiyambi.

"Ndipo anadza ku Nazarete, kumene analeredwa; ndipo tsiku la Sabata analowa m'sunagoge, monga anazolowera, naimiririramo kuwerenga m'kalata." – Luka 4:16.

Chizolowezi cha Yesu chikhale chathu; chifukwa Iye ali chitsanzo chathu. "Iye wakunena kuti akhala mwa Iye, ayeneranso mwini wake kuyenda monga anayendera Iyeyo.' 1 Yoh. 2:6.

"Nakusiyirani chitsanzo kuti mukalondole mapazi ake." 1 Petro 2:21.

"Ine ndasunga malamulo a Atate wanga, ndipo ndikhala m'chikondi chake." Yoh. 15:10.

"Pakuti ichi ndi chikondi cha Mulungu, kuti tisunga malamulo ake." 1 Yoh. 5:3

M'nthawi yake yakukhala padziko, Yesu chitsanzo chathu anamvera Malamulo Khumi.

Nauzanso ophunzira ake kusunga Malamulowo.

"Musaganize kuti ndinadza Ine kudzapasula chilamulo kapena aneneri: sindinadza kupasula, koma kukwaniritsa. Pakuti indetu ndinena kwa inu, Kufikira litapirira thambo ndi dziko, kalemba kakang'ono kamodzi kapena kansonga kake kamodzi sikadzachokera kuchilamulo, kufikira zitachitidwa zonse. Chifukwa chake yense wakumasula limodzi la malangizo amenewa ang'onong'ono, nadzaphunzitsa anthu chomwecho, adzatchulidwa wamng'onong'ono…" Mateyu 5:17-19.

Liu la Chihelene (pleroo) m'ndime yapamwambayi limatanthauza "kukwaniritsa" kapena " kukhala chitsanzo changwiro" kapena "kudzadzilitsa," monga lafotokozedwa m'ndime yotsatirayi: "Izi ndalankhula ndi inu, kuti chimwemwe changa chikhale mwa inu, ndi kuti chimwemwe chanu chidzale." – Yohane 15:11; Yohane 16:24; Afil. 2:2.

Liu la Chihelene [Greek ) lomwelo latchulidwanso. Apa silikutanthauza kuti chimwemwe chanu chingaonongedwe (katalusai), koma kuti chimwemwe chanu chikhala chodzadza, champhamvu ndi chakuya (pleroo).

Pleroo pa Akolose 1:25 ndi ("wakukwaniritsa mau a Mulungu,") pa 2 Akorinto 10:6 ndi ("kumvera kwanu kudzakwanitsidwa.").

Monga Yesu sasinthika, malamulo ake sangasinthenso. Palibe kukonzanso malamulo ndi malangizo oyendetsera mtundu wa anthu, komwe Atate Wakumwamba akuchitenso chilengedwere dziko lapansi. Umulungu ndi wangwiro, nchifukwa Mulungu akudzudzula kusayeruzika kwa munthu poyesera kusintha malamulo Ake.

"Koma andilambira Ine kwachabe, ndikuphunzitsa maphunzitso malangizo a anthu." Mateyu 15:9.

"Ndipo inu mupeputsa mau a Mulungu chifukwa cha miyambo yanu." Mateyu 15:6.

"Inunso mupeputsiranji lamulo la Mulungu chifukwa cha miyambo yanu?" Mateyu 15:6. Khristu anachita zonse monga mwa Malemba ndipo pakutero "Anachikuza chilamulo ndi kuchilemekeza."

"Chinakondweretsa Yehova chifukwa cha chilungamo chake kukuza chilamulo, ndi kuchilemekeza." Yesaya 42:21.

"Pamenepo ndinati, Taonani, ndadza; M'bukhu mwalembedwa za Ine: kuchita chikondwero chanu kundikonda, Mulungu wanga. Ndipo malamulo anu ali mkati mwamtima mwanga." Masalmo 40:7-8. (yerekezani ndi Ahebri 10:5, 7).

Iye anachita ichi pamaso pa mbadwo wokhotakhota, wochimwa ndi wogarukira – monga inachitiranso mibadwo ina.

Khristu analimbikitsa anthu olungama kumvera Malamulo a Mulungu monga Iye:

"Si yense wakunena kwa Ine, Ambuye, Ambuye, adzalowa mu Ufumu wa Kumwamba; koma wakuchitayo chifuniro cha Atate wanga wa Kumwamba." Mateyu 7:21.

"Chifukwa chake yense wakumasula limodzi la malangizo amenewa ang'onong'ono, naphunzitsa anthu chomwecho, adzatchulidwa wamng'onong'ono mu Ufumu wa Kumwamba; koma yense akuchita ndi kuphunzitsa awa, iyeyu adzatchulidwa wamkuru mu Ufumu wa Kumwamba." Mateyu 5:19.

"Mphunzitsi wabwino, chabwino nchiti ndichite, kuti ndikhale nao moyo wosatha? Ndipo Iye anati kwa iye…Koma ngati ufuna kulowa m'moyo, sunga malamulo." Mateyu 19:16-17. Patokha tiribe mphamvu yakuchita chifuniro cha Mulungu, mwa chisomo cha Khristu ndimo.

"Ine ndine mpesa, inu ndinu nthambi zake: wakukhala mwa Ine, ndi Ine mwa iye, ameneyo abala chipatso chambiri; pakuti kopanda Ine simungathe kuchita kanthu." Yohane 15:5.

M'phunziro la ("Pemphero Loiwalika,") tamva kuti Yesu anauza ophunzira ake kupitiriza kusunga Sabata la m'Baibulo, - tipitirizenso kuchichita ichi ku nthawi zonse kufikira chimaliziro (Mateyu 24:20). Anthu ochuruka amati, Sabata linathera pa Gologotha, ndipo Mulungu sanafuna munthu kusunganso lamulo'li. Amati Malamulo Khumi anathera pa mtanda!

Poyankha funso lakuti, "Ndiye kuti palibe malamulo ali onse oyendetsera Chikhristu?" Ena amayankha, "Palibe ngakhale lamulo limodzi. Yesu anathetsa onse, ndipo ife sitisowanso kusunga ngakhale limodzi. Chikondi chalowa m'malo mwakusunga Malamulo. Anthu osokonekera maganizowa amati isanachitike imfa ya pa mtanda, anthu analamulidwa kusunga Malamulo Khumi kuti asachimwe; koma Mulungu anatuma Mwana wake, kuti anthu adzikhala mu uchimo ndi kupulumutsidwa ali m'uchimo momwemo. Maganizo amenewa sachikhristu! Mulibe chiphunzitso cholakwika chotere m'Malemba.

"Ndipo adzabala mwana wamwamuna, ndipo udzamutcha dzina lake Yesu; pakuti Iyeyo adzapulumutsa anthu ake ku machimo ao." Mateyu 1:21.

Izi ndi zina za zomwe Mulungu analankhula za kufunikira kwa kusunga Malamulo Ake:

"Mau atha; zonse zamveka zatha; opa Mulungu, musunge malamulo ake; pakuti choyenera anthu onse ndi ichi. Pakuti Mulungu adzanena mlandu wa zochita zonse, ndi zobisika zonse, ngakhale zabwino ngakhale zoipa." Mlaliki 12:13-14.

"Yense wakuchita tchimo achitanso kusayeruzika; ndipo tchimo ndilo kusayeruzika." 1 Yohane 3:4.

"Pakuti uchimo udziwika ndi lamulo." Aroma 3:20.

"Pakuti mphotho yake ya uchimo ndi imfa." Aroma 6:23.

"Pamenepo tidzatani? Kodi chilamulo chiri uchimo? Musatero ai. Komai ne sindikadazindikira uchimo, koma mwa lamulo ndimo; pakuti sindikadazindikira chilakolako sichikadati chilamulo, Usasirire." Aroma 7:7.

"Potero kodi lamulo tiyesa chabe

mwa chikhulupiriro? Musatero ai; koma [ndi chikhulupiriro] tikhazikitsa lamulo." Aroma 3:31.

"Pakuti amene ali yense angasunge malamulo onse, koma akakhumudwa [akachimwa] pa limodzi, iyeyu wachimwira onse. Pakuti Iye wakuti, Usachite chigololo, anatinso, Usaphe. Ndipo ukapanda kuchita chigololo, koma ukapha, wakhala wolakwira lamulo." Yakobo 2:10-11.

"Pakuti ichi ndi chikondi cha Mulungu, kuti tisunge malamulo ake: ndipo malamulo ake sali olemetsa." 1 Yohane 5;3.

"Kuopa Yehova ndiko chiyambi cha nzeru; onse akuchita chotero ali nacho chidziwitso chokoma; chilemekezo chake chikhalitsa kosatha." Masalmo 111:10.

"Ngati inu muli ofuna ndi omvera, mudzadya zabwino za dziko." Yesaya 1:19.

"Akukonda chilamulo chanu ali nao mtendere wambiri; ndipo alibe chokhumudwitsa." Masalmo 119:165.

"Mwenzi utamvera malamulo anga mtendere wako ukanakhala ngati mtsinje, ndi chilungamo chako monga mafunde a nyanja." Yesaya 48:18.

"Pakuti akumvaimva lamulo sakhala olungama pamaso pa Mulungu, koma akuchita lamulo adzayesedwa olungama." Aroma 2;13.

"Komai ye wakupenyerera m'lamulo langwiro, ndilo laufulu, natero chipenyerere, ameneyo, posakhala wakumva wakuiwala, komatu wakuchita ntchito, adzakhala wodala m'kuchita kwake." Yakobo 1:25.

"Umo tizindikira kuti tikonda ana a Mulungu, pamene tikonda Mulungu ndi kuchita malamulo ake." 1 Yohane 5:2.

"Pano pali chipiriro cha oyera mtima, cha iwo akusunga malamulo a Mulungu, ndi chikhulupiriro cha Yesu." Chibvimbulutso 14:12.

Ndi chilamulo cha Malamulo Khumi chomwe oyera mtima ayenera kuchisunga. Pamene anafunsidwa "Malamulo Khumi ati?" Yesu anayankha potchulapo angapo a Malamulo Khumiwo (Mateyu 1917-19). Mtumwi Yakobo anachitanso chimodzimodzi (Yakobo 2:10-11).

Anthu akuti malamulo anasiya kugwira ntchito pa imfa ya Khristu. Bukhu Lopatulika likuti ngati palibe lamulo ndiye palibenso uchimo! Ndi zoona, ngati palibe malamulo nanga uchimo ungadziwike ndi chiyani?

"Koma pamene palibe lamulo pamenepo palibe kulakwa." Aroma 4:15.

"Koma uchimo suwerengedwa popanda lamulo.' Aroma 5:13.

"Pakuti uchimo udziwika ndi lamulo." Aroma 3:20.

"Komai ne sindikadazindikira uchimo, koma mwa lamulo ndimo." Aroma 7:7.

"Yense wakuchita tchimo achitanso kusayeruzika; ndipo tchimo ndilo kusayeruzika." 1 Yohane 3:4.

Malamulo omwe anathetsedwa pa mtanda ndi a chilamulo cha zinsembe chakutchulapo malangizo. Malamulowa anali malangizo a kaperekedwe ka zinsembe koyenera kufikira pa nsembe ya Khristu. Choncho pambuyo pa imfa ya Khristu alibedi ntchito chifukwa nsembe zophera za nkhosa m'Kachisi zinalekeka; - Khristu Nkhosa yathu anatifera. – ,tikuuzidwa kusunga Malamulo Khumi, ngakhale pambuyo pa imfa ya Khristu.

Daneli 9:26-27 analosera kuti imfa ya Khristu "adzaleketsa nsembe yophera ndi nsembe ya ufa." Paulo akuti izi zinachitikadi atangofa Khristu. Malamulo otchulapo malangizo a zinsembe anathetsedwa. Mautumiki a zinsembe a m'Kachisi anakwanitsidwa m'nsembe ya Khristu nasiya kukhala a tanthauzo kwa Mulungu.

"Adatha kutifafanizira cha pa ifecho, cholembedwa m'zoikikazo, chimene chinali chotsutsana nafe: ndipo anachichotsera pakatipo, ndikuchikhomera ichi pa mtanda." Akolose 2:14.

"Atachotsapo udani m'thupi lake, ndiwo mau a chilamulo cha kutchulapo malangizo…." Aefeso 2:15-16.

Mlembi wa chi-Protestant, Dr Albert Banes pochitira ndemanga Akolose 2:16 anati:

"Koma kugwiritsa ntchito kwa liu ["masabata"] mochurukitsa, zikuonetsa kuti iye [Paulo] amanena za chiwerengero chachikuru cha masiku omwe anasungidwa mu zikondwerero za Chihebri, ndipo zinali mbali ya malamulo a mautumiki a zinsembe – osati Lamulo Losasinthika lomwe ndi Malamulo Khumi. Palibe liri lonse la Malamulo Osasinthika – Malamulo Khumi – linanenedwa kuti liri "mthunzi wa [zinthu] zinarinkudzazo.'" – Dr Albert Banes, Commentary on Colossians 2:16.

"Malamulo a mthunzi wa zirinkudza" anali nankungwi wotilozera ku nsembe ya Khristu: kuphera kwa nkhosa ndi mbuzi, kusunga kwa masiku a zikondwerero, ndi zina. Onsewa anathetsedwa pa imfa ya Khristu.

"Pakuti chilamulo, pokhala nao mthunzi wa zokoma zirinkudza…sichitheka kuti mwazi wa ng'ombe zamphongo, ndi mbuzi ukachotsera machimo." Ahebri 10:1-4.

M'malamulo a zinsembe munalinso masiku oyera otchedwanso "masabata" a pa chaka ndi a zikondwerero. Malamulowa anaperekedwa munthu atachimwa pakuswa Malamulo Khumi momwe muli la Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri Anali chomtetezera wochimwayo ku imfa ndi chilango cha Mulungu. Chifukwa chakuti Ayuda anachita zinsembezi mosayenera, Khristu nsembe ya ngwiro anaperekedwa kudzatetezera mtundu wa anthu monga mwa zifundo za Mulungu. Choncho zinsembe ndi malamulo ake zimaimira nsembe yopanda chirema ya Khristu. M'mautumiki amenewa mumachitika nsembe " za nyama" ndi "za zomwaimwa." Masabata a zikondwererowa akupezeka pa Levitiko 23:4-44. M'Bukhu Lopatulika Sabata la pa mulungu la masiku asanu ndi awiri limangotchedwa "Sabata" pomwe masabata a zinsembe akufotokozedwa liri lonse ndi cholinga cha utumiki wake. Pokhala ochuruka, masabata a zinsembewa amatchulidwa mochurukitsa kuti "masabata" kapena "masiku a sabata." Paulo akuti onsewa anathera pa mtanda chifukwa anali "mthunzi" wa zinalinkudza kutanthauza oimira nsembe yakudziperekа m'malo mwa ochimwa ya Khristu.

"Chifukwa chake munthu ali yense asakuweruzeni inu m'chakudya, kapena chakumwa, kapena m'kunena tsiku la phwando, kapena tsiku lokhala mwezi, kapena masiku a sabata; ndizo mthunzi wa zirinkudzazo; koma thupi ndi la Yesu." Akolose 2:16-17.

"Pakuti chilamulo, pokhala nao mthunzi wa zokoma zirinkudza, osati chifaniziro chenicheni cha zinthuzo, sichikhozatu, ndi nsembe zomwezi chaka ndi chaka, zimene azipereka kosalekeza, kuwayesera angwiro iwo akuyandikira." Ahebri 10:1.

Kuti tchito ya zinsembe ndi masabata ake zinathera pa imfa ya Khristu, chinatsimikizika pomwe dzanja losaoneka lakumwamba linang'amba pakati chinsaru chotchinga cha m'Kachisi pa tsiku lakuphedwa kwake:

"Ndipo Yesu, pamene anapfuula ndi mau akuru, anapereka mzimu wake. Ndipo onani, chinsaru chotchinga cha m'Kachisi chinang'ambika pakati kuchokera kumwamba kufikira pansi." Mateyu 27:50-51.

"Pamenepo ndinati [Ine Khristu], Taonani ndafika (Pamutu pake pa bukhu palembedwa za Ine) kudzachita chifuniro chanu, Mulungu…Nsembe ndi zopereka ndi nsembe zopsereza zamphumphu ndi za kwa machimo simunazifuna…Achotsa choyambacho, kuti akaike chachiwiricho." Ahebri 10:7-9.

Malamulo a mthunziwa anakwanitsidwa m'imfa ya Khristu, kuti mwa iyi Iye alimbikitse, khalidwe lakumvera ndi kusunga Malamulo Khumi a Mulungu – mwa chisomo cha Khristu munthu apatsidwe mphamvu yakulakika!

Tikakangamira pa Khristu, Iye adzatichotsera machimo ndi kutipatsa mphamvu yamoyo waumulungu wangwiro.

Tikadza kwa Iye ndi mtima wobvomereza ndi wolapa, tidzakhulukidwa ndi kuyesedwa "olungama kwaulere, ndi chisomo chake, mwa chiombolo cha mwa Khristu Yesu." Aroma 3;24. Choncho, tiyeni, tiyende ndi Khristu ndi kukhala moyo mwa Iye. Timsankhe Iye pozisiya njira zathu zakale za uchimo.

"Chifukwa chake tidzatani? Tidzakhalabe m'uchimo kodi, kuti chisomo chichuruke? Musatero ai. Ife amene tiri akufa ku uchimo, tidzakhala bwanji chikhalire m'menemo?" Aroma 6:1-2.

"Ngati musunga malamulo anga mudzakhala m'chikondi changa." Anatero Yesu –Yohane 15:10.

Tikatsegula nkhokwe za Malemba ndi Mbiri ya dziko – zonse ziwiri zikufotokoza choonadi za kusiyana kwa Sabata la Malamulo Khumi ndi masabata a zinsembe. Zolemberazo zikusiyanitsanso Sabata loona ndi Sunday motere:

Tsiku la Sabata lachisanu ndi chiwiri ndi lokhalo loyera la pa mulungu lomwenso Mulungu analipatsa ku mtundu wa anthu kwamyaya. Sunday ndi longopanga munthu.

M'mutu wotsatirawu muli mpfundo zochokera m'Baibulo zokhuza Sunday, tsiku loyamba:

## *KOMA SIZINACHITIKEPO*

Kodi munthu angasinthe tsiku lake lobadwira nkuliika pa lina? "Nzosatheka."

Khristu sasintha. Analenga dziko lapansi popanda. Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri ndi chizindikilo cha mphamvu yake yakulenga, ndiyakuti ali Mlengi yekhayo woyenera kumlambira. Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri linapatsidwa ndi Mulungu kwa munthu likhale chikumbutso cha kulengedwa kwa miyamba ndi dziko lapansi, silinasinthe – ngati padakhalapo kusintha, kukanayambira kuchiyambi kuchilengedwe! Kutanthauza kuti ngakhale mulungu wakulenga, uli pa Genesis 1, ukanasinthidwanso. Mulungu akanafafaniza zonse ndi kuyambiranso mwatsopano.

Anthu ena amatsutsa kuti dziko silinalengedwa. Komatu ndi kutsutsako sangakuchotse kulengedwako: dziko lapansi ndi zinthu zonse ziri m'menemo linalengedwa m'masiku asanu ndi limodzi, ndipo tsiku lachisanu ndi chiwiri Mulungu Mlengi anapumula, nalipatula ndi kuliyeretsa limenelo.

Lamulo la Sabata la m'Bukhu Lopatulika silopepuka kuti munthu angangolisintha monga akufunira. Ndi chizindikilo chachikuru choulozera mtundu wa anthu kuchipembedzo choyera cha Mulungu Mlengi.

M'munsimu ndi zina za zomwe a Mpatuko ena odziwika ananenapo pokanitsitsa za kusintha kwa Sabata:

"Chifukwa chomwe lamulo la [Sabata] linaperekedwera – nchakuti likhale chikumbutso kuti Mulungu anapumula atalenga zonse – silinasinthe kuchoka pa lachisanu ndi chiwiri kukhala pa lina liri lonse; palibe chingadzetse kusintha kuli konse ngati Mulungu sanalamulire kutero [m'Malemba]– kaya kuuka kwa akufa kwa Ambuye Yesu kapena china

chiri chonse…

"Pakuti ife, amene tiri pansi pa Uthenga Wabwino, tingapembedze moyenera, ngati titatsatira zolembedwa m'Malamulo Khumi – ndipo chingakhale chokoma kusunga tsiku lachisanu ndi chiwiri molingana ndi momwe Mau a Mulungu akunenera, kuposa kulemekeza tsiku lina [loyamba la pa mulungu] pongotsanzira ndi kumvera ulamuliro wa umunthu." John Milton, A Posthumous Treatise on the Christian Doctrine, Book 2, Chapter 7 (John Milton [1608-1674] anali Mlakatuli wotchuka wa Chingelezi ndiponso Mlembi bukhu lotchedwa ("Pradise Lost").

"Ngatidi chilamulo (cha Malamulo Khumi) chiripo, tiyeni tichisunge ichi…Koma ngati kulibe, tiyeni tisiyenso ngakhale kusunga modzinyenga tokha tsiku lina liri lonse m'malo mwake. 'Inde,'anthu ena amati Sabata linasintha kuchoka pa tsiku lachisanu ndi chiwiri kupita pa loyamba. Linasinthidwira kuti? Liti? Ndi ndani? Silinasinthidwe, ndipo sizidzatheka , pokhapokhapo chitasinthidwanso chilengedwe choyambacho.

"Nkhani yakusintha kwa Sabata kuchoka pa tsiku lachisanu ndi chiwiri kupita ku tsiku loyamba, 'ndi nkhambakamwa ' yongopeka.'.Ngati linasinthidwadi, ndiye kuti kunachitidwa ndi ulamuliro wa iye amene ananenedwa kuti adzayesetsa kusintha nthawi ndi chilamulocho [Danieli 7:25] kapena atumiki ake. Ndikuganiza dzina lake ndi Kachenjede [Dr] Wokanakhristu [Antichrist]'" – Alexander Campbell, "The Christian Baptist," February 2, 1824, Vol. 1,, No. 7. Campbell [1788-1866] anali wa Mpatuko wa chi-Irish, yemwe anakhazikitsa mpingo wotchedwa Ophunzira A Khristu [Disciples of Christ]).

Anthu angalankhule zambiri zakukulemekeza kuuka kwa Khristu kwa akufa popita ku nyumba zopemphererako pa Sunday m'mawa, nkumapumula pa tsikuli. Koma chodziwika ndi chakuti kugwira ntchito pa tsiku la chisanu ndi chiwiri – tsiku lomwe limatsatidwa ndi la Sunday, - ndi kuswa lamulo Lachinai. Choonadi chake ndi chimenecho. Kodi ife timvere maganizo athu kapena Mau ndi chifuniro cha Mulungu? Lero anthu akusunga Sunday potsanzira akhristu oukira Mulungu a ku Alexandria ndi Romu omwe anasunga tsiku'li pofuna kukondweretsa mulungu wa Dzuwa ndi ompembedza ake kuposa kulemekeza Mulungu.

Ngati munthu akudziwa kuti Bukhu Lopatulika likulimbikitsa kusunga ndi kupembedza pa Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri, – koma iye nkumapembedzabe pa Sunday – akuchimwira Lamulo Lachinai! Woteroyo pokana kuchita lamulo la Mulungu, akumvera lamulo la munthu!

Funso: Kodi m'Chipangano Chatsopano palipo pakutiuza kusunga Sunday loyera? Liripo lemba likupereka ulamuliro wosintha la Sabata loyera kuchoka pa tsiku lachisanu ndi chiwiri kukhala pa loyamba?

Palibe lemba ndi limodzi m'Bukhu Lopatulika lomwe likuchitira umboni za kusinthaku.

Palibe m'Bukhu Lopatulika pomwe Sunday latchedwapo lopatulika, Sabata kapena tsiku la Ambuye.

Sunday latchulidwa kasanu ndi kanai m'Bukhu Lopatulika. Koyamba pa Genesis 1:5, pomwe panenedwa za tsiku loyamba la mulungu wakulenga. Langofotokozedwa monga limodzi la masiku asanu ndi limodzi a ntchito osati lopatulika.

Kasanu kena Sunday latchulidwa mokhuzana ndi kuonekera kwa Yesu kwa ophunzira ake pambuyo pa kuuka kwake m'manda atapumula pa la Sabata la m'Bukhu Lopatulika (Mat. 28:1; Mk 16:1-2, 9; Lk 24:1; Jn 20:1, 19). Yesu anadza kwa ophunzira ake ndi kuwauza uthenga wabwino, kuti anali moyo. Palibe umboni uli wonse wa kupatulidwa kwa Sunday.

Malemba asanu ndi atatu a Chipangano Chatsopano momwe Sunday latchulidwamo:

Mateyu 28:1 lemba loyamba: Likungotiuza kuti la Sabata limatsatidwa ndi tsiku loyamba la mulungu. – Mateyu analemba mau'wa pambuyo pa zaka makumi angapo Khristu atauka komanso atakwera kale Kumwamba.

Marko 16:1-2 lemba lachiwiri, Marko 16:9 lachitatu: Malemba awiriwa akuti la Sabata linali litadutsa pomwe limayamba tsiku loyamba. Ndipo la Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri ndi lopatulika; linzakelo ndi limodzi la masiku asanu ndi limodzi a ntchito. Zaka zambiri zinapitapo kuchokera pomwe Khristu anauka, Marko akananenapo za kuyeretsedwa kwa Sunday.

Luka 24:1 lemba lachinai: Luka akuti okhulupirira ena a Yesu "anapumula monga mwa lamulo" (Lachinai la Eksodo 20:8-11). Nayambanso zokadzoza thupi la Yesu pa Sunday. Likungopitiriza kufotokoza kwa Lk 23:55-56. M'moyo wake Yesu sanaphunzitsepo za chiyero cha Sunday – ophunzira ake sanalisungepo. Kupatulidwa kwa Sunday ndi chachilendo m'Malemba.

Yohane 20:1 lemba lachisanu: Likuti kuuka kwa Yesu kunachitika tsiku loyamba [Sunday] m'mbanda kucha.

Yohane 20:19 lemba lachisanu ndi chimodzi: Yohane akuti ophunzira anasonkhana chipinda chimodzi "chifukwa chakuopa Ayuda" ndipo Yesu anawaonekera kuwalimbikitsa. Sikuti ophunzirawo anali pamsonkhano wakupembedza. Anali ndi mantha kuti mwina angagwidwe ndi kuphedwanso monga zinachitikira ndi Yesu. Anthu ena amati pa nthawiyi ophunzira amakondwerera za kuuka kwa Khristu. Sizoona, chifukwa pomwe amasonkhana pamalo obisalawo nkuti asanadziwe kuti Khristu anauka. Marko akutsimikizira ichi pakunena kuti, ophunzirawa sanamvetsetse za chinachitikacho. Mk 16:11 ndi 16:12-13). Ndipo pamene Khristu anaonekera kwa iwo (Lk 24:33-37) zinawatengera nthawi kukhulupirira kuti analidi Iye.

Machitdwe 20:7-8 lemba lachisanu ndi chiwiri: Atakhala masiku asanu ndi awiri ku Trowa, madzulo amenewo, Paulo ndi gulu lake anasonkhanitsa okhulupirira kutsazikana nao komwe kunafika mkati mwa usiku. ( M'kawerengedwe ka m'Baibulo) tsiku loyamba la pa mulungu limayamba Saturday madzulo, dzuwa likangolowa, ndipo limatha dzuwa likangolowanso madzulo otsatira. Choncho msonkhano wa pa Machitidwe 20:7-11, unayamba pakulowa kwa dzuwa kwa Saturday komwe kunali kuyamba kwa tsiku loyamba [Sunday], m'kawerengedwe ka lero tikanati unali "Usiku wa Saturday kuchera Sunday." Msonkhano unayamba m'maora a tsiku loyamba la mulungu, komwe kunali kulowa kwa dzuwa kwa Saturday. Ikanakhala kuti inali m'nthawi yomwe ife timatcha "usiku wa Sunday," tikanati unachitika usiku wochera tsiku lachiwiri [Monday].

"Anali madzulo pakutha kwa la Sabata la Chiyuda pakuti m'mwawa [Sunday] chingalawa chomwe akwere chinati chinyamuke." – Conybeare and Huwson, Life and Epistles of the Apostle Paul, Vol. 2, p. 206. (Mbiri ya Mtumwi Paulo).

"Ayuda amawerenga tsiku kuchokera madzulo mpaka m'mawa, potsatira kawerengedweka tsiku loyamba la pa mulungu limayamba madzulo dzuwa litangolowa pa Saturday. Alembi ambiri, akugwirizana pakuti mtumwi Paulo anayembekezera maora a la Sabata athe, kenaka nkuyamba msonkhano wotsazikana ndi okhulupirira a ku Trowa… madzulo dzuwa litalowa pa Saturday, nanyamuka ulendo wake Sunday m'mawa." – Dr. Horato B. Hackett, Commentary on Acts, pp. 221-222. (Dr Hackett anali Mphunzitsi wa Chipangano Chatsopano m'Chihelene pa Rochester Theological Seminary.)

Utangotha msonkhano ku Trowa .. (Machitidwe 20:7-11) gulu la Paulo lokhala kale m'maora a ntchito, linanyamuka usiku womwewo. Paulo anasankha kuyenda yekha mbali ina ya ulendowo, ndipo m'mawa wa tsikulo [Sunday], anali atayenda zipumulo khumi, zisanu ndi zinai kulowera ku Assosi, komwe abwenzi ake anamkweza chingalawa (Machitidwe 20:11-14).

Ngati Sunday linali lopatulika kwa Paulo, anakhaliranji iye ndi okhulupirira a ku Trowa masiku asanu ndi awiri, ndi kunyamuka pa Sunday'lo m'mawa ndi cholinga chakuti ayende zipumulo khumi zisanu ndi zitatu ndi theka pa tsikulo? Bukhu Lopatulika likuti, "umu ndimo iye anakonzetsera" za ntchito anati achite pa Sunday.

Iwo anakhala masiku asanu ndi awiri ku Trowa, ndipo usiku wa Saturday kuchera Sunday (Sabata litatha) anasonkhanitsa ndi kulawirana ndi okhulupirira, "popeza anati achoke m'mawa mwake." Kunyema mkate, siunali utumiki wa mgonero? Kunyema mkate kumatanthauzanso kudya chakudya wamba. "Ndipo tsiku ndi tsiku.. ananyema mkate kunyumba kwao" (Machitidwe 2:46), "nalandira chakudya ndi chisangalalo" (2:46). Ngakhale okhulupiririrawa akanachita utumiki wa mgonero usikuwo, sikunali kulipanga Sunday kukhala lopatulika. Mgonero wa Ambuye ungathe kuchitidwa nthawi iri yonse, ndiponso tsiku liri lonse (1 Akorinto 11:26). Mgonero wa Ambuye ndi chikumbutso cha imfa ya Khristu, osati cha kuuka kwake, "mulalikira imfa ya Ambuye kufikira akadza Iye." (Ndime 26).

M'bukhu la Machitidwe monganso Mateyu, Marko, Luka, Yohane ndi ena mulibe za kupatulika kwa Sunday.

1 Akorinto 16:1-2 ndi lemba lachisanu ndi chitatu ndi lotsirizanso kutchula za tsiku loyamba la mulungu m'Chipangano Chatsopano, ndi lokhalo m'zolembera za Paulo.

Paulo anafunsa okhulupirira kusunga pambali ndalama zothandizira osauka ku Yerusalemu. Iye anati zopereka zisonkhanitsidwiretu osati akadzafika kapena m'utumiki wa la Sabata. "Kuti zopereka zisachitike pakudza ine" – koma munthu aliyense monga anadalitsidwira m'kati mwa mulungu,"Yense wa inu asunge yekha."

Kaperekedwe kotereka ka zopereka sikakukhuzana ndi zopereka za mulungu uli wonse m'mautumiki akupembedza. Tiphunzire ife kumapatuliratu ndalama za ntchito ya Mulungu ku nyumba zathu tsiku ndi tsiku kuyambira pa tsiku loyamba monga momwe tadalitsidwira; kutero kumapeputsa zochitika pa Friday (tsiku lachisanu ndi chimodzi) masana chifukwa cha kuchepa kwa nthawi yokonzekera Sabata lomwe limayamba dzuwa likangolowa. Kuwerengera ndalama ndi kupatula zopereka zathu pa la Sabata ndi kuipysa maora opatulika a tsiku'li.

M'malemba asanu ndi atatu momwe Sunday likutchulidwamo m'Chipangano Chatsopano – mulibe za kuyeretsedwa kwa tsiku latsopano, mulibe umboni wakupatulidwa kwa tsiku lina, kulowa m'malo mwa la Sabata lachisanu ndi chiwiri.

Tiyamike Mulungu potipatsa Bukhu Lopatulika! Liri njira yotitsogolera kwa Khristu ndi kumoyo wosatha. Tiyende m'menemo osati m'ziphunzitso za zolakwika mabodza a anthu odzinamiza kuti ndi ophunzira. Tizikanitsitse zimenezo.

Anthu ena amati ngakhale palibe lamulo lakuti tidzisunga Sunday – Chibvumbulutso 1:10 likutitsimikizira kuti tidzisunga tsiku loyamba la pa mulungulo m'malo mwa tsiku la chisanu ndi chiwiri.

"Ndinagwidwa ndi Mzimu tsiku la Ambuye, ndipo ndinamva kumbuyo kwanga mau akuru, ngati lipenga." Chibvumbulutso 1:10.

Lembali ndi ndime zolitsatira silikutchulapo Sunday; koma langoti "Tsiku la Ambuye."

Tiyerekeze lemba'li ndi ena onena za "Tsiku la Ambuye" m'Bukhu Lopatulika. Koma tisanafike konseko tikumbukirenso kuti Yohane anakhala ndi Yesu muutumiki Wake wonse wa m'dziko lapansi, ndipo amadziwa bwino chomwe tsiku la Ambuye limatanthauza. Kwa zaka zitatu iwo anasunga la Sabata la pamulungu; monganso mwachizolowezi Yesu anasunga Sabata la m'Baibulo'li.

"Ndipo tsiku la Sabata analowa m'sunagoge, monga anazolowera, naimiriramo kuwerenga m'kalata." Luka 4:16.

Wophunzira wokondedwayu anamumva Yesu akuphunzitsa kuti Iye [Yesuyo] ali "Ambuye ngakhale wa tsiku la Sabata" (Mat. 12:8; Mk 2:28).Yohane anakumbukiranso kuti m'Chipangano Chakale Mulungu analankhula mobwerezabwereza zakuti tsiku la chisanu ndi chiwiri ndi la Sabata la Yehova. Choncho nkosatheka kuti Yohane potchula "Tsiku la Ambuye," amatanthauza Sunday [tsiku loyamba] – motsutsana ndi Malaemba!

"Tsiku la Ambuye" ndi limodzi lokha; lachisanu ndi chiwiri – la Sabata la m'Baibulo. Werengani Yesaya 58:13

"Ukaletsa phazi lako pa Sabata, ndi kusiya kuchita kukondwerera kwako TSIKU LANGA LOPATULIKA…"

"Tsiku la Ambuye" lopatulika ndi ndi liti? Tsiku lachisanu ndi chiwiri ndilo la Ambuye:

1. Sabata la m'Baibulo ndi tsiku lopatulika la Yehova (Ek. 16:23, 25; 31:15; 32:2).

2. Sabata la m'Baibulo ndilo la Sabata la Yehova (Ek. 20:10; Lev. 23:3; Deut. 5:12, 14).

3. Sabata la m'Baibulo ndi Sabata lake; Yehova akulitcha ili "tsiku langa lopatulika." (Yes. 58:13).

4. Sabata la m'Baibulo ndilo Yesu anati ali Ambuye wa ilo (Mat 12:8; Mk 2:28).

Ndi mau "Tsiku la Ambuye," (Chibvumbulutso 1:10 ) Yohane sankatanthauza Monday, Thursday, kapena Sunday!

Yohane amadziwa bwino lomwe liri Tsiku la Ambuye, la Sabata la chisanu ndi chiwiri: ndipo linaikidwa likhale lachikumbutso la Mlengi (Gen. 2:1-3; Ek. 31:17. Nilikhalanso Lachikumbutso cha Kupulumutsa (Ezek. 20:12, 20).

Kukonda Mulungu ndiko kumvera ndi kuchita Mau ndi Malamulo ake. Satana samakondwera ndi ichi, amafunitsitsa ataononga kotheratu ubale wa munthu ndi Mulungu. Tiri m'nthawi ya kumapeto komwe atsogoleri ambiri a chipembedzo atangwanika ndi chiphunzitso chakuti Malamulo Khumi ndi osafunika, anathetsedwa pa mtanda. Kutero ndi machenjerero a Satana ndipo aneneri a Mulungu analosera kale kuti adzachitika:

## *KUKWANIRITSA ULOSI*

Danieli anakhalapo m'modzi wa atsogoleri m'ufumu wa Babulo kwa zaka 51. M'chaka cha 553 B.C., ali m'tulo anaonetsedwa masomphenya – zirombo zinai zoopsya zikuturuka m'nyanja, chimodzi pambuyo pa chinzake, ndi kuima m'mphepete mwa nyanjayo. Ali kusinkhasinkha tanthauzo la masomphenyawo, Mulungu anamfotokozera Danieli kuti zirombo zinaizo zinali maufumu anai otsatizana a dziko lapansi omwe adzauka:

"Chaka choyamba cha Belisazara mfumu ya Babulo Danieli anaona maloto, naona masomphenya a m'mtima mwake pakama pake; ndipo analemba lotolo, nalifotokozera, mwachidule. Danieli ananena, nati Ndinaona m'masomphenya anga usiku, taonani, mphepo zinai za mumlengalenga zinabuka pa nyanja yaikuru. Ndipo zinaturuka m'nyanja zirombo zazikuru zinai zosiyanasiyana." Danieli 7:1-3.

Mngelo anamasulira loto la Danieli motere:

M'mutu wachiwiri wa bukhu la Danieli, ndi ulosi womwe ukukhuza mbiri ya dziko kuchokera nthawi ya Danieli kufikira Kubwera Kwachiwiri kwa Khristu.

M'chizindikilo cha fano lokhala m'mitobvu yosiyanasiyana (Dan. 2:31-35) maufumu akuuka wina pambuyo pa unzake. Kuyambira ndi ufumu wa Babulo womwe unaimiridwa ndi mutu wa golide, womwenso umalamulira m'nthawi ya Danieli (Dan. 2:38), mpaka zaka za mtsogolo, za maufumu omwe anatsatira: wa Amedi-Aperezi, Ahelene, Aroma ndi nyanga zake khumi zogawikana (Dan 2:39-43) mpaka ufumu wa zala za kumapazi ndi zala – wa nthawi yathu ino – pomwe Khristu akubwera ku dziko lapansi kudzatenga olungama kunka nao kumwamba (Dan. 2:44-45).

Patapita zaka 50 Danieli anaonetsedwanso masomphenya ena a ulosi a Danieli 7: omwe anafanananso katanthauzidwe ndi a Danieli 2, koma mwakuyako.

M'lotoli m'malo mwa mitobvu ya fano, zinali zirombo zinai (Dan 7:2-3). Chirombo chachinai chinali ndi "nyanga yaing'ono" yomwe pakuphuka inazula nyanga zitatu. Kuopsa kwa nyanga yaing'ono kunakopa chidwi cha Danieli.

"Patsogolo pake zitatu za nyanga zoyambazi zinazulidwa ndi mizu yomwe; ndipo taonani, m'nyanga m'menemo munali maso ngati maso a munthu, ndi pakamwa palikunena zazikuru.

"Pamenepo ndinafuna kudziwa choonadi cha chirombo chachinai chija chinasiyana nazo zonsezi, choopsya chopambana, mano ake achitsulo, ndi makabado ake amkuwa, chimene chidalusa, ndi kuphwanya, ndi kupondereza zotsala ndi mapazi ake; ndi za nyanga khumi zinali pamutu pake, ndi nyanga yina idaphukayi, imene zidagwa zitatu patsogolo pake; nyangayo idali ndi maso ndi pakamwa pakunena zazikuru, imene maonekedwe ake anaposa zinzake." Dan. 7:8, 19-20.

Danieli anakhuzidwa ndi mphamvu ya nyanga yaing'onoyi yomwe inali m'kuuka m'ulamuliro wa chirombo chachinai: Nyanga yaing'ono ndi bungwe loopsya lakhala likuyesetsa kuononga anthu ndi kusintha Malamulo a Mulungu.

"Ndinapenya, ndipo nyanga yomweyi inachita nkhondo ndi opatulikawo, niwalaka, mpaka inadza Nkhalamba ya kale lomwe; ndi mlandu unakomera opatulika a Wam'mwambamwamba, nifika nthawi yakuti ufumu unali wao wa opatulikawo.

"Anatero, chirombo chachinai ndicho ufumu wachinai pa dziko lapansi, umene udzasiyana nao maufumu onse, nudzalusira dziko lonse lapansi, nudzalipondereza ndi kuliphwanya.

"Koma za nyanga khumi, m'ufumu uwu adzauka mafumu khumi, ndi pambuyo pao idzauka yina; iyo idzasiyana ndi oyamba aja, nidzachepetsa mafumu atatu." Danieli 7:21-24.

Zoipitsitsa zomwe zakhala zikuzichitidwa ndi nyanga yaing'ono ndi kutalika kwa nthawi yomwe inazichitira izi:

"Nidzanena mau akutsutsana ndi Wam'mwambamwamba, nidzayesa kusintha nthawizo ndi chilamulo; ndipo adzaperekedwa m'dzanja lake mpaka nthawi imodzi, ndi nthawi zina, ndi nthawi yanusu." Danieli 7:25.

1. Ulamuliro wa nyanga yaing'ono unalamulira dziko lapansi kwa zaka 1260. Yotchedwa: "Nthawi ndi nthawi zina ndi nthawi yanusu" (Dan. 7:25); "Miyezi makumi anai mphambu iwiri" ya Chibvumbulutso 11:2, ndipo "masiku chikwi chimodzi, mazana awiri mphambu makumi asanu ndi limodzi" a pa chibvumbulutso 12:6. Ulamuliro wa ufumu wa nyanga yaing'ono unafotokozedwanso m'maina osiyanasiyana m'maulosi angapo. Tsiku limodzi m'ulosi wa m'Baibulo limaimira chaka chimodzi (Num. 14:34; Ezra 4:6); choncho masiku 1,260 ndi zaka 1,260. "Nthawi," m'ulosi imaimira chaka chimodzi (Dan. 11:13, Revised Version); choncho "nthawi ndi nthawi zina ndi nthawi ya nusu" ndi zaka chaka chmodzi, ziwiri ndi theka la chaka, - zaka zitatu ndi theka. Nthawiyi ndi chimodzimodzi miyezi 42. Ndipo nthawi ziwirizi zingofanana ndi ya ulosi wa masiku 1,260 kapena zaka 1,260. M'kawerengedwe ka chi-Yuda, chaka chiri ndi masiku 360 kapena miyezi 12 ya masiku 30 uli wonse. Nyanga yaing'ono inalamulira ndi kuzunza miyoyo ya anthu kwa zaka zoposera chikwi.



2. Mbiri ya dziko ikuti Ulamuliro wa nyanga yaing'ono unalandira mphamvu yake ku ulamuliro wa chirombo chachinai, - wa Aroma wachikunja, pomwe ukamapita kumapeto. "Nyanga" khumi za ulamuliro wachikunjawo zinali maulamuliro khumi ogawanika: Asanu ndi awiri anali Anglo-Saxons (England walero), Afrank (France walero), Alombard (Italy walero), Alemanni (Germany walero), Abergundian (Switzerland walero), Asuevi (Portugal walero) ndi Avisigoth (Spain walero). Atatu asakupezeka pa mndandandawu anali Aheruli, Avandal ndi Aostrogoth omwe anafafanizidwa pakuphuka kwa nyanga yaing'ono.

3. Nyanga yaing'ono unali ufumu monga anali maufumu ena patsogolo pake (Dan 7:24). Unachokera m'ulamuliro wa chirombo chachinai (Ufunu wa Aroma Wachikunja). Unakhala pambuyo pakuuka nyanga zinazo nuthetsa nyanga zina zitatu pozizula ndi mizu yomwe (Dan. 7:24).

Ufumu wa nyanga yaing'onoyo "unasiyana" ndi enawo. (Dan. 7:24). Unali wophatikizana chipembedzo ndi ndale ndipo unalamulira amitundu kwa zaka mazana mazana.

4. Ulamuliro wa nyanga yaing'ono unali ndi maonekedwa ngati munthu:

"Ndipo taonanai, m'nyangamo munali maso ngati maso a munthu, ndi pakamwa palikunena zazikuru." Dan. 7:8.

Unachita chipongwe Mulungu ndi amitundu.

Ulosi wa Chibvumbulutso 13 ufotokozanso za ulamuliro wachipongwe:

"Ndipo chinatsegula pakamwa pake kunena zamwano pa Mulungu, kuchitira mwano dzina lake, ndi chihema chake, ndi iwo akukhala m'Mwamba." Chibv. 13:6.

Ulosi wa Chibvumbulutso 13:1-8 ukugwirizana ndendende ndi wanyanga yaing'onon wa Danieli 7.

"Nidzanena mau akutsutsana ndi Wam'mwambamwamba." Dan. 7:25.

Ulamulirowu, unasiyanadi ndi ena – utsogoleri wake unatsutsana ndi Mulungu

kufikira podzitcha wokha Mulungu!

5. Ulamulirowu ukupitirizabe kuchitira nkhanza anthu a Mulungu okana ziphunzitso zake.

"Ndinapenya, ndipo nyanga yomweyi inachita nkhondo ndi opatulikawo, niwalaka." Dan. 7:21.

Baibulo likuti ulamulirowu ukuyesetsa kuononga olungama pa nkhope ya dziko ndi kusokoneza choonadi..

"Nidzanena mau akutsutsana ndi Wam'mwambamwamba, nidzalemetsa opatulika a Wam'mwambamwamba, nidzayesa kusintha nthawizo ndi chilamulo." Dan. 7:25.

Upapa ndi ulamuliro womwe ukukwaniritsa zonsezi. Danieli 7 akugwirizananso ndi Chibvumbulutso 12 mpaka 17, ulamulirowu pouonetsera kuti unazunza anthu a Mulungu kwa nthawi ya zaka 1260.

6. Ulamulirowu unayesetsa kusintha Malamulo a Mulungu kukwaniritsa mau akuti:

"Nidzanena mau akutsutsana ndi Wam'mwambamwamba, nidzalemetsa opatulika a Wam'mwambamwamba, nidzayesa kusintha nthawizo ndi chilamulo." Dan. 7:25.

Kufotokoza Mwachidule:

Mpingo wa Katolika wayesetsa kuchotsa Lamulo Lachiwiri la Malamulo Khumi, loletsa kupembedza mafano. Waligawa Lamulo la Khumi pawiri pofuna kukwanitsabe chiwerengero cha Malamulo Khumi motere: ("Usasirire nyumba yake ya mbale wako" ndi "Usasirire mkazi wake wa mbale wako." Wayesetsa kuchotsa la Sabata pa tsiku lachisanu ndi chiwiri - Saturday - ndi kuliika pa tsiku loyamba – Sunday. Onse okana kutsatira chiphunzitso cha sabata la bodzali akhala akuzunzidwa ndi kuphedwa. (Dan. 7:8, 20-21, 25; 8:9-12). Ulosi wakuti ulamuliro wa nyanga yaing'ono udzayesera kusintha nthawi ndi chilamulo uli pa Danieli 7:25.

"Nidzanena mau akutsutsana ndi Wam'mwambamwamba, nidzalemetsa opatulika a Wam'mwambamwamba, nidzayesa kusintha nthawizo ndi chilamulo." Dan. 7:25

Ndi Mulungu yekha anayenera kusintha Malamulo omwe ndi chikhalidwe chake, osati munthu. Koma Mtumwi Paulo analosera kuti munthu wakusayeruzika ndiye adzayesera kusintha Malamulo Khumi ndi kudzitcha Mulungu.

"Munthu asakunyengeni konseko; kuti silifika, koma chiyambe chifike chipatukocho, nabvumbulutsidwe munthu wosayeruzika, mwana wa chiononongeko, amene atsutsana nazo, nadzikuza pa zonse zotchedwa Mulungu, kapena zopembedzeka; kotero kuti iye wakhala pansi ku Kachisi wa Mulungu, nadzionetsera yekha kuti ali Mulungu." 2 Atesalonika 2:3-4.

Ulamuliro wa upapa waika munthu wolengedwa kuti adzipatsidwa ulemu woyenera Mulungu – [kupembedzedzwa] m'Kachisi m'malo mwa Mulungu, wasintha Malamulo a Mulungu nubvomereza kuti Sunday ndi CHILEMBA/CHIZINDIKILO cha ulamuliro wake.

Koma zachitikadi momwemo? Ulamuliro uli wonse wodzinena kuti uli ndi mphamvu yakusintha Chilamulo cha Mulungu – uyenera kukhala Mulungu amene! – ndi Mulungu yekha ali ndi mphamvu ya kusintha Malamulo Ake.

Mulungu ndi munthu ndi zinthu ziwiri zolekana. Munthu ndi cholengedwa cha moyo waufupi; Mulungu ndi Mlengi ndi wamyaya. Malamulo a Muyaya a Mulungu ali maziko pomwe pakhazikikapo ulamuliro wake. Zolengedwa zonse za dziko lapansi ziyenera kumvera Malamulo ake omwe Iye wazipatsa. Pasakhale cholengedwa choyesera kusintha Malamulo Khumi.

Ine ndilemekeze ulamuliro wa Mulungu pakuchita chifuniro chake ndi kulimbikitsa anthu enanso kutero. Ndisadzilekanitse ndi Mulungu ndikudzikhalira moyo ndekha pakunyalanyaza ndi kukana kusunga malamulo ake. Ndisadzipange kukhala mulungu wina, podzipangira malamulo otsutsana ndi a Mulungu – ndisalimbikitse anthu ena kusunga malamulo a eni okha m'malo mwa omwe Mulungu analamulira tonse kuwasunga!

Malemba akuti yense wokana kumvera Mulungu adzikhalira kapolo wa mwini yekha:

"Kodi simudziwa kuti kwa iye amene mudzipereka eni nokha kukhala akapolo ake akumvera iye." Aroma 6:16.

Ngati timvera Mulungu, tikhala atumiki ake. Koma ngati timvera munthu – tikhala akapolo a munthuyo.

Momwe tazindikira ichi, tisachedwe,tisinthe makhalidwe mwamsanga.

Mau a Mulungu akuti kumvera munthu, posunga malamulo ake otsutsana ndi a Mulungu – mwadala ndi kuchimwa – kumeneko sikupembedza Mulungu, Mlengi, wa kumwamba ndi dziko lapansi - napumula pa Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri, – koma kupembedza munthu, malamulo ndi bungwe lake. Kulemekeza malamulo osinthidwa ndi munthu tikulemekeza cholengedwa m'malo mwa Mlengi.

Ndi ulamuliro wa nyanga yaing'ono yokha womwe pokhala ngati walochedwa ndi chitsulo cha moto walimbitsa mtima kusintha Malamulo a Mulungu. Ndipo mosadzitsutsa ukupitiriza kudzitamandira…pobwerezabwereza… kawiri kawiri.

## *KUDZITAMANDIRA KUTI UNASINTHADI MALAMULO*

Nkofunika kuwakumbutsa a mipingo ya chi-Presbyterian, chi-Baptist, chi-Methodist ndi a chikhristu ena kuti Bukhu Lopatulika silikuwabvomereza kulilemekeza Sunday. Sunday ndi la Mpingo wa Katolika, ndipo onse olilemekeza akulemekeza lamulo la Mpingo wa Katolika." (Priest Brady, m'zolankhula zake ku Elizabeth, N.J. pa macrch 17, 1903, ndi kufalitsidwa m'Nyuzi ya Elizabeth N.J.ya March 18, 1903. Zokonzedwa ndi Kelly Mbusa wa Chikatolika Catholic University of America).

"Papa ali ndi mphamvu, ndipo wakhala akuigwiritsa iyi ntchito posintha ena a malamulo a Khristu….Chomwe Papa wachiganiza sichimalakwika. Angathe kutsutsa ndi kukonza cholakwika kukhala chokhoza, pakukonzanso kapena kusintha malamulo.". – Zochokera m'nthawi ya Pope Nicholus.

"Ampatuko…amapembedza pa Sunday m'malo mwa Saturday, lomwe akudziwa linasinthidwa ndi Mpingo wa Katolika… Sakuganiza iwo kuti analandira Bukhu Lopatulika, ndipo polemekeza Sunday, ndiye kuti akubvomereza ulamuliro wa uneneri wa Mpingo, wa Papa." - Our Sunday Visitor, February 5, 1950, (Imodzi ya Magazine Za Chikatolika Yotchuka m'U.S.).

"Momwe ziriri Ampatuko angofunika kusankhapo chimodzi cha ziwiri izi: kusunga Saturday lopatulika kapena Sunday lopatulidwa ndi Chikatolika. Koma nkosatheka kuchita zonse." – The Catholic Mirror, December, 23, 1893. (Mirror ndi Nyuzi ya pa mlungu ya Chikatolika).

"Mapfuko onse a chikhristu aika chilemekezo chao pa Mpingo wa Katolika, maboma ambiri akhazikitsa malamulo okakamiza kusagwira ntchito ndi kupembedza pa Sunday. Ampatuko, omwe anaturuka mu Mpingo'wu, alibe chifukwa cholemekezera Sunday, ndi ayenera iwo kusunga Saturday monga Sabata. Pokhazikitsa malamulo osunga Sunday kukhala Loyera, boma likubvomereza ulamuliro wa Mpingo wa Katolika, ndi zikhazikitso zake. Chiyero cha Sunday, monga tsiku lopembedza Mulungu Wakumwamba ndi chikhakhazikitso osati cha wina ali yense koma cha Mpingo wa katolika." – John Gillmary Shea, in The American Catholic Quarterly Review, January 1883, p. 139. (Shea [1824-1893] anali katswiri wotchuka wa Mbiri ya Chikatolika).

"Papa si nthumwi ya Yesu kokha, koma Yesu Khristu Mwini wake, m'thupi la umunthu." The Catholic National, 1895.

"Mpingo wa Katolika…ndi mphamvu zake zokhala utumiki wa Mulungu, unasintha tsikuli kuchoka Saturday kukhala Sunday." The Catholic Mirror, September 23, 1893, ya Chikatolika ya pa mulungu m'Baltimore (yobvomerezedwa ndi Cardinal Gibbons).

"Funso: – Kodi, a Mpanduko akamaipsya [kugwira ntchito wamba] Saturday, tsiku lachisanu ndi chiwiri, akutsatira Malemba okhawo monga maziko a chikhulupiriro chao – kapena akutsutsana ndi Bukhu Loyera?

Yankho: – Asadzinamize. Poipsya Saturday, komwe nkuswa limodzi la malamulo a Mulungu, lomwe liri chikhalire langwiro, - 'Uzikumbukira kusunga tsiku la Sabata loyera, iwo akuchita miyambo ya anthu [Katolika] ..'" – Priest Steven Keenan, A Doctrina Catechism, pp. 252,254. (Katekesimo wa Wansembe wa chi-Skotiwu akugwiritsidwa ntchito m'sukulu za Chikatolika kuwaphunzitsira ana zikhulupiriro za Upapa.)

"Tikanatsatira Baibulo lokha, tikanakhala tikusungabe tsiku la Sabata lopatulika, lomwe ndi Saturday." - John Laux, A course in Religion for Catholic High Schools and Academies, 1936 edition, Vol. 1, p.51. (J. J. Laux [1878-1939] anali wansembe wa Chikatolika, mphunzitsi ndi mlembi wa Mbiri za Chikatolika ndi anthu ao oyera mtima.)

"Nkofunika kumakumbukira kuti kusunga Sunday – lomwenso Ampanduko aliyesanso lopembedza lao – kulibe umboni wa m'Baibulo kokhako, koma ndi kutsutsana ndi Baibulo'lo, lomwe limalamulira za mpumulo wa la Sabata, lomwe ndi Saturday. Ndi Mpingo wa Katolika womwe, ndi mphamvu zopatsidwa ndi Yesu Khristu, unasinta mpumulowu, kuuika pa Sunday." – Monsignor Louis Segur, Plain Talk About the Prostetantism of Today, p. 213. (L.G. Segur [1820-1881] anali wansembe wa chi-Fransa, yemwe pambuyo anasankhidwa kukhala woimira za Malamulo m'Romu.)

"Maina onse omwe Khristu amadziwika nao m'Malemba, pokhala Iye Mutu wa Mpingo, ndi omwenso papa amatchulidwa nao." – Robert Cardinal Bellarmine, De Conciliorum Auctoriatate ( (On the Authority of the Councils,) Bk 2, chap. 17. (Bellmine [1542-1621], mphunzitsi wamkuru ndi mtsogoleri ku Jesuit Gregorian University, m'Romu, yemwe anali wotsogola wa aphunzitsi onse ophunzitsa ma-Jesuiti m'mbiri ya bungweli.)

"Sunday ndi CHIZINDIKILO cha ulamuliro wathu! – Mpingo uli pamwamba pa Baibulo, ndipo kusintha kwake Sabata ndi umboni wa ichi." – The catholiv Record, London. Ontario, Canada, September 1, 1923.

Alembi onse a mbiri ya dziko akugwirizana kuti kuyesetsa kusintha Sabata la m'Baibulo kukhala Sunday kunachitika Baibulo litalembedwa kale.

"Mpingo wa Katolika ukubvomera mobwerezabwereza, ndikudzitamandira, mosabisa kuti ndiwo, osati Mulungu, kapena alembi a Baibulo – [Vatican] unakuchita kusinthaku.

A Mpanduko akubvomerezanso kuti kusinthaku sikochokera m'Baibulo:

"Pakhala pali lamulo losunga tsiku la

Sabata, lomwe si la Sunday. Inde, ena akhala akudzitamandira kuti anasintha Sabata ndi zonse zomwe zimachitika pa tsikuli kuchokera pa tsiku lachisanu ndi chiwiri ndi kuziika pa tsiku loyamba la pa mulungu. Momwe ndafufuzira ine kwa zaka zambiri, funso ndi lakuti: Kodi umboni wakusinthaku ukupezeka pati? Chifukwa m'Chipangano Chatsopano – mulibe. Mulibe umboni uliwonse M'malemba wakusintha Sabata kuchoka tsiku lachisanu ndi chiwiri kukhala pa loyamba.

"Palibenso paliponse pomwe Yesu anakambiranapo ndi ophunzira ake zolichotsa Sabata kumiyambo yoipa [ya Chiyuda], ndi kulika pa tsiku lina; komanso kuti m'masiku makumi anai atauka kwa akufa sanalamulire ichi. Mzimu Woyera ndiye sanalamulirenso kutero. Ngakhale mipingo [wa Atumwi], siunaphunzitsepo kapena kulamulira ziwalo zake za kusinthaku.

" Ndafunanso nditsindike kuti Sunady silinasungidwepo ngati la Sabata ndi Atate Oyambirira a Mpingo wa Chikhristu. Silikutchulidwa konse monga tsiku lakupembedza mu mbiri ya Chikhristu ndi zolembera zina. Tsiku'li likulumikizidwa ndi mulungu wa Dzuwa kotero kuti madzedwe akenso m'chikhristu ndi achikunja pokhala ilo chizindikilo chachikunja, ndipo linalandiridwa ndi kuyeretsedwa ndi machitidwe a oukira Mulungu a upapa, ndi kuphunzitsidwa ngati loyera kwa a Mpanduko. Dr E. R. Hiscox, Mlembi wa Baptist Manual. Zochokera m'zolembera za Dr Hiscox.

Palibe maumboni ambiri kuchokera kwa Ampanduko koma malo sakulora kuti onsewo alembedwe:

British Congregationists: "Ngakhale tililemekeze bwanji Sunday, sitikusunga la Sabata...Sabata linakhazikitsidwa pa malamulo oikika a Mulungu. Silingasinthidwe mwachisawawa kukhala pa Sunday.. Palibe m'Chiapangano Chatsopano ndime yoti tidzalangidwa ngati osalilemekeza Sunday.' Dr R.W. Dale, The Ten Commandments , Hodder and Stoungton, pp. 106-107.

Protestant Episcopal: "Funso – M'Chipangano Chatsopano, liripo lamulo losintha Sabata la Saturday kukhala pa Sunday?"

Yankho: "Palibe." Manual of Christian Doctrine, p. 127.

American Congregationists: "Chiphunzitso chatsopano chakuti Khristu ndi ophunzira anapereka ulamuliro wakuika tsiku loyamba kukhala lakupumula m'malo mwa lachisanu ndi chiwiri chiribe umboni m'Chipangano Chatsopano." Dr Layman Abbot, in the Christian Union, June 26, 1890.

English Independent: "Sabata m'Chihebri ndi mpumulo, ndi tsiku lachisanu ndi chiwiri la mulungu,..ndi tibvomereze kuti m'Chipangano Chatsopano mulibe lamulo la chiyero cha tsiku loyamba." – Charles Buck, A Theological Dictionary, art. "Sabbath," p. 403. (Buck [1777-1815] anali mbusa ndi mlembi.)

Methodist Episcopal: "Sabata ndi lapachilengedwe linatsimikizidwa ndi Mose ndi aneneri mobwerezabwereza, silinasinthidwepo pokhala limodzi la Malamulo Khumi, palibe kalemba kapena kansongа kake kamodzi kachotsedwapo." Bishop's Pastoral, 1874 edition.

Christian Church (Christian Connection): "Mpingo wa Aroma..unasintha lamulo lachinai poyesetsa kuthana ndi Sabata la m'Mau a Mulungu, nuika Sunday kukhala lakupumula." Nicholas Summerbell, History of the Christian Church, 3rd ed., 1873, p. 415. (Smmerbell [1816-1889] anali Mtsogoleri wa Union Christian College m' Indiana.)

Disciples of Christ: "Palibe umboni m'Malemba wotsimikizira za tsiku loyamba kuti ndi "Tsiku la Ambuye." - Dr D.H. Lucas, in the Christian Oracle, January 23, 1890.

Baptist: Palibe m'Malemba pomwe pakulitchula tsiku loyamba la mulungu kuti Sabata..Palibe ngakhale ulamuliro wakutero kuchokera m'Malembawo." – The Watchman.

Episcopal: "Sabata linakhala lakupembedza mu mpingo Wakum'mawa zaka mazana atatu zapitazo ndiponso pambuyo pa imfa [yowawitsa] ya Mpulumutsi wathu." – Prof. E. Brerewood of Gresham College, London, in Sermon.

Anglican: "Ndi pati m'Malemba pomwe pakuti tidzisunga tsiku loyamba? Tikuuzidwa kusunga tsiku lachisanu ndi chiwiri; palibe pomwe pakutiuza kusunga tsiku loyamba. Chifukwa chimene tikusungira tsiku loyamba kukhala lopatulika m'malo mwa lachisanu ndi chiwiri ndi kufuna kwathu kulemekezera zinthu zina osati kuchokera Baibulo, mpingo, ndiwo watero [watilamulira]." Isaac Williams, Plain Sermons on the Catechism, Vol. 1,pp. 334, 336.

Methodist: "Ndi zoona kuti palibe lamulo lakuti ana akhanda azibatizidwa. Chomwechonso palibe lamulo loti tidzisunga tsiku loyamba la mulungu. Anthu ambiri amaganiza kuti ndi Khristu anasintha Sabata, Koma kuchokera m'Mau ake, zikuoneka kuti sanadze kudzasintha chilamulo. Ngati anthu ena amatero nzongopeka." – Amos Binney, Theological Compedium, 1902 edition, pp. 180-181, 171. (Binney [1802-1878] anali mbusa wa Methodist ndi mlangizi, amene zolembera zake zinafalitsidwa kwa zaka makumi anai m'zilankhulo zambiri, yemwe analembanso Methodist New Testament Commentary.)

Southern Baptist: "Palibe ulamuliro uli wonse wakusintha Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri la Chiyuda kukhala l la Chikhristu loyera la tsiku loyamba…

"Mulibe lamulo m'Chipangano Chatsopano, ganizo, kapena ndondomeko za kapembedzedwe zolimbikitsa chiyero cha Tsiku La Ambuye [Sunday].

Palibe kugwirizana kuli konse [kulumikizana] komwe kulipo pakati pa Sabata la Ayuda ndi la Chikhristu la Tsku la Ambuye.. Ili linadza m'kanthawi kochepa amitundu atayamba kuchuruka [m'mpingo woyambirira] wa Chikhristu. Iwo anadza ndi ziphunzitso zao za chikunja zomwe mkati mwake munali cha Dzuwa – magwero a Sunday." William Owen Carver, Sabbath Observance, 1940, pp. 49, 52, 54. (Dr Carver [1868-1954] anali mphunzitsi wamkuru wa phunziro loyerekeza zipembedzo ku Southern Baptist Theological Seminary, ku Louisville Kentuky.)

Episcopalian: Kulilemekeza tsiku loyamba m'malo mwa lachisanu ndi chiwiri kukudalira pa Mpingo wa Katolika, wa Katolika wokhawo." – Hobart Church News, July 2, 1894.

Irish Methodist: "Palibe umboni kuti Sabata linathetsedwe, kapena kuti mphamvu yake inachotsedwa chifukwa cha Chikhristu [m'zaka za pambuyo]. Ndafotokoza pena pake kuti, 'Uzikumbukira tsiku la Sabata likhale lopatulika,' ndi lamulo lamyaya." – Adam Clark, The New Testament of our Lord and Saviour Jesus Christ, Vol. 2, p. 524. (Clark [1760-1832] anali mbusa, mlembi ndi nasankhidwa katatu kukhala mtsogoleri wa Methodist Conference.)

Southern Baptist: "Momwe ziri m'Malemba Sabata silinapangidwe ndi mtsogoleri ali yense wachipembedzo. Si liri mbali iri yonse ya mchitidwe wa chipembedzo, koma chinthu cha pachokha. Genesis likuti ndi chimodzi cha zoyamba kulengedwa, chopatulidwa ndi Mlengi Mwini wake." – W.O. Carver, Sabbath Observance, pp.40-41. (Dr Carver [1868-1954] anali mphunzitsi wamkuru wa phunziro loyerekeza zipembedzo ku Southern Baptist Theological Seminary, ku Kentucky.)

Zolemberazi ndi za chilendo kwa ife.

Choyamba. Zingatheke bwanji munthu wolengedwa kusintha tsiku lopembedzera loikika ndi Mulungu (maziko a chipembedzo cha m'Baibulo cha Mulungu wakumwamba) ndi kuliika pa tsiku lina?

Chachiwiri, zingatheke bwanji kuti munthu wolengedwayo aumirize anthu onse kutsatira kusintha kwakeko?

Kachitatu, zikutheka bwanji kuti anthu omwe m'nthawi ino akudziwerengera okha Baibulo akupitiriza kubvomereza cholakwikacho pakupitiriza kusunga tsiku lopembedzera Dzuwa?

Chifukwa chiyani Akonzanso a Mpanduko a zaka za m'ma 1500 sanabwezerenso kusunga Sabata?

Nthawi inawachepera yoti nkukonza zolakwika zonse. Aroma anawatangwanitsa ndi kuwagonjetsa atsogoleri a Kukonzanso. Otsatira a okonza anayendanso m'mapazi a atsogoleri ao, Luther ndi Calvin.

Nanga nchifukwa ninji Vatican sakulapa za kusintha komwe iwo ndi Constantine anakuchita? Bwanji osatsogolera akhristu kubwerera ku Sabata la m'Baibulo?

Kusintha kunachitikaku ndi maziko pomwe pamangika Mpingo wa Katolika. Ndi chizindikilo cha ulamulio Mpingowo – kubvomereza kulakwa kungakhale kupereka ulamuliro wa chipembedzo chake kwa Mulungu Mwini Sabata loona.

## *CHIZINDIKIROCHO CHAMANGIDWANSO*

Chipilala chofiira cha mwala ngati nsanja chamangidwa.

Chipembedzo cha Katolika wa Aroma chafika pachimake tsopano. Chipilala chofiira cha Vatican chamangidwa pakati chapatsogolo pa Chalichi cha Petro Woyera. Pakatikati pa makoma akuru 280 olochedwa-m'makongoletsedwe aluso (omwe mtemgo wake m'pafupifupi myanda umodzi wa ndalama za chi-America [a million dollars]) pakuima chipilara cha maonekedwe ofiira-ngati dzuwa. Chikulemera matani 320, chotalika mapazi 83 kukwera kumwamba, chokhala ndi maziko mapazi 42 pamwamba pake – choimikidwa pa malo okwaniria mapazi 132.

Chipilala chachikuru ngati ichi, chinamangidwapo m'Heliopolis, "Mzinda wa Dzuwa," m'Aigupto wakale. Lero chikuima patsogolo pa Basilica Papale di San Pietro in Vaticano – St Peter's Bisilica palikuru la chipembedzochi, Vaticak – Mzinda watsopano wa Dzuwa.

Pa October 31, 1517, Martin luther anakhoma chikalata cha mpfundo 95 zotsutsa pa khomo la Chalichi cha Sukulu ya Ukachenjede m'Wittenberg, Germany. Ichi chinali chiyambi cha Ampanduko Akukonzanso Kwakukuru.

Koma Kukonzanso'ko sikunachite chipambano chifukwa Luther ndi anzake anali atangoturuka mu mdima wa zolakwika za mpingo wa Katolika, choncho anali ndi kuunika kochepa kosati nkukonza zolakwika zonse. Tithokoze Mulungu pachomwe amachiyamba anthu akewa, kwinaku tikuzindikira kuti ndi udindo wathu kuitsiriza ntchito imene anaiyambayi.

Pamene Kukonzanso kunafika ku Ulaya m'zaka za m'ma 1500, Aroma anayesetsa kukutchinga pakusokoneza malingaliro a anthu za chipembedzo cha m'Baibulo. Iwo anagwiritsa njira zitatu: kuthetseratu Upanduko, Machitidwe a upandu a ma-Jesuiti komanso Msonkhano wa Trent.

Msonkhano wa Trent unaitanitsidwa ndi Papa nuyamba pa December 13,

1545 mpaka December 4, 1563. Cholinga cha msonkhanowo chinali kumveketsa ziphunzitso za Mpingo wa Katolika ndi kuulimbikitsa Mpingowo pa nkhondo yake yolimbana ndi Apanduko. Unali umodzi wa misonkhaono yopambana kwambiri mu mbiri ya Aroma.

Ampanduko ananka akulalikira kuti chiphunzitso chiri chonse chidziyezedwa ndi Mau a Mulungu. Ndipo chikapezeka choperewera chikanidwe. Choonadi.chi ndicho chinali maziko a Upanduko.

Koma Aroma analimbana nacho nachisokoneza ndi kuwabwezera anthu m'ukapolo wa uchimo. Munali magawano mu mpingowo. Chobetchera chachikulu pakati pa nthumwi za msonkhano chinali chakuti kodi mpingo upitirize kukweza miyambo kuposa Bukhu Lopatulika. Mpingo wa Katolika wakhala ukumanga uzimu wake pa maziko a ziphunzitso za umunthu ("Miyambo"), koma pozibisa izi m'Malemba. Iwo akhala akuphunzitsa kuti miyambo iposa Mau a Mulungu pa chitsutsano, chiphunzitso, ndi machitidwe ena onse a uzimu.

Kodi "Miyambo" ndi chiyani? Ndi ziphunzitso malangizo a anthu. Ndi ndondomeko zopangidwa m'misonkhano ya Mpingo wa Katolika, malamulo a apapa, ndi mau olankhulidwa ndi akufa omwe mpingowo umati ndi oyera.

"Ngati mitsinje iwiri yoturuka m'Paradiso, Baibulo ndi Miyambo ziri Mau a Mulungu, ngale zonyezimira za choonadi.

"Ngakhale mitsinje iwiri ya umulunguyi, gwero lake ndi lofanana m'chiyero, iri kuunika kwa choonadi, koma, mwa iwiriyo, MIYAMBO kwa ife [akatolika] ndi yopambana [kuposa Malemba]." – Joseph F. Di Bruno, Catholic Belief, 1884 ed., p. 45.. (Di Bruno anali wansembe ndi mlembi wa Chikatolika wa chi-Italiana).

Pamene msonkhano wa Trent unayamba, panali kulimbana za chiphunzitsochi. Kodi Miyambo ipose Baibulo kapena ziwirizi zitengedwe kuti nzofanana ulamuliro? Kodi Baibulo litengedwe kukhala la mphamvu ndi kuti miyambo ithetsedweretu?

Ampanduko anadzudzula kwambiri za uchikunja wa zikhulupiriro za upapa – zomwe zinakhazikika pa miyambo maphunzitso a anthu. Popeza miyambo ya Mpingo wa Katolika sinali ziphunzitso zolamitsa koma maneno osokonekera ndi osokoneza, panakhala kusiyana maganizo a episcopi ndi otsatira ao ku Trent, kunakhala kobvuta kuti angolengeza kuti anasankha Miyambo kukhala maziko a chikhulupiriro cha Mpingo wa Katolika. Kenaka kangofika kamzimu kokhala ngati kolekerera – nkudzanso kongodzidzimutsa.Palibe china unali mkangano wa tsiku limodzi Sabata lakupembedza.

Kenaka Gaspar de Fosso, m'episkopi wamkuru wa Regio, anaimirira ndi kulankhula pa January 18, 1562, ndi kupereka chigamulo chomwe chinamanga tsogolo la Ukatolika mpaka lero lino.

Pongoima iye, onse anatchera makutu, ndipo iye analankhula ndi mtima wake wonse kuyamikira Miyambo, nadzudzula onse ananyozetsa miyambo ya mpingowo.

Ambiri analankhula kale zotchinjiriza Miyamboyo, ndi chiyaninso china kuposa del Fosso kumangirira zonse? Iye anati Mpingo wa Aroma unakhazikika pamaziko Miyambo ndi Maphunzitso a anthu; ndipo sungakhale popanda chiphunzitsochi. Anaizamitsa mpfundoyi pozifotokozera nthumwi za msonkhanowo kuti chitsimikizo chakuti chiphunzitso cha "Miyambo chiposa cha m'Malemba" ndiponso ndi choona, m'zaka za mbuyomo, Mpingo wa Aroma unasintha Sabata la tsiku la chisanu ndi chiwiri lomwe Mulungu mwini wake analikhazikitsa ndi kuilika pa Sunday tsiku loyamba.

Del Fosso anati ICHI ndi chitsimikizo kuti Miyambo iposa Baibulo – chifukwa Mpingo wagwiritsa ntchito miyambo kusintha malamulo okhazikitsidwa ndi Mulunguy ndipo ichi chachitika mwa chipambano! Ndipo kuposa apo, del Fosso anapitiriza – Ampanduko akulemekeza Mpingo wa Aroma posunganso Sunday. M'mawa umenewo, del Fosso analankhula mwachimvekere kuti chiyero cha Sunday chinali korona wachipambano cha chiphunzitso cha Chikatolika.

Kulankhula kwa Del Fosso kunathetsa mkangano wonse. ( Mukufotokoza kwake Del Fosso anatinso "muli monse tingachitire ziribe kanthu." Kutanthauza kuti "Ndingathe kuchita chiri chonse cholakwika pokhala palibe chondiletsa." – Kaganizidwe komwe nkauchimo kosachokera m'Mau ndi chitsogozo cha umulungu woona koma mzimu woukira.

Apatu nkuti pafupifupi zaka makumi atatu, usanachitike msonkhao wa Trent, atsogoleri a Mpanduko atangotulutsa Chibvomerezo chao ku Msonkhano wa Augsburg kuti Mpingo wa Katolika ndiwo unayesetsa kusintha Sabata la m'Baibulo:

"Iwo [a episkopi a Chikatolika] akuti asintha Sabata kukhala "Tsiku la Ambuye" motsutsana ndi Malamulo Khumi; koma kungolankhula pakamwa za kusinthako. Ndiye kuti Mpingowu uli ndi mphamvu zochuruka! pofika pothetseratu la Sabata!

"Koma za kusinthako, tingofotokoza momveka kuti a espiskopi alibe mphamvu yakusintha chiri chonse motsutsana ndi Uthenga Wabwino monga…" From the Augsburg Confession, quoted in Library of Original Sources, Vol. 5, pp.173-174.

A Mpanduko atangoonetsa mbali yomwe chikhulupiriro chao chinali ku Augsburg, Germany, m'1530, Okanzanso ndi owatsatira ao anapezeka ali m'khondo ya chizunzo: kumenyera chikhulupiriro chao – komanso miyoyo yao - ichi chinawatangwanitsa kuti sanathe kupitiriza ntchito ya Kukonzanso – zina zoiwalika za choonadi cha m'Baibulo chomwe chinaponderezedwa ndi ziphunzitso za bodza m'zaka zambuyo.

Koma atsogoleri a Chikatolika amazindikira za Sabata loona – ndipo akutiuza m'zolembera zao:

"Sunday ndi chiphunzitso cha Chikatolika, ndipo chiyero ndi kasungidwe kake zingathe kutchinjirizidwa ndi malamulo a Chikatolika..M'Malemba mulibe ndime ndi imodzi yomwe ikubvomereza za kusintha kwa kapembedzedwe, kuyambira tsiku lotsiriza mpaka loyamba la mulungu." – Catholic Press, Sydney, Australia, August 1900.

"Tikuwakumbutsa a Presbyterians, Baptist, Methodist, ndi magulu ena a Chikhristu, kuti Baibulo silikuwabvomereza konse kusunga Sunday. Sunday ndi lokhazikitsidwa ndi Mpingo wa Katolika, ndipo iwo amene amasunga ili, akusunga lamulo la Mpingo wa Katolika." – Priest Brady, in address at Elizabeth, NJ., on March 17, 1903.

"A Mpanduko amanyoza ulamuliro wa Miyambo ya Chikatolika, nati akukhulupirira Baibulo, Baibulo lokha; koma akutsatira miyambo ya Mpingo wakalewo yomwe mulibe m'Baibulo, nkumapumula pa tsiku la Miyambo la mpingowo! Lamulo lofunikira kwambiri la Malamulo Khumi limati 'Uzikumbukira tsiku la Sabata likhale lopatulika'.. Tsiku la Sabata, lomwe Mulungu anati lidzisungidwa, ndi Saturday . Ndi angati mwa Akatolika ndi a Mpanduko kupatula timagulu tiwiri, akusunga lamulo ili? Palibe! Chifukwa? Koma Baibulo lomwe amati akulimvera kwatunthu sikupereka ulamuliro uli wonse za kusunga tsiku loyamba la mulungu m'malo mwa lachisanu ndi chiwiri. Nanga iwo akuutenga kuti ulamuliro wakutero? Iwo akulemekeza ndi kumvera ulamuliro wa Mpingo wa Katolika, womwe anaupandukira." John L. Stoddard, Rebuilding a Lost Faith, p. 80. (Stddard [1850-1931] anali wokana Mulungu ndi mlembi m'moyo wake wonse kumapeto m'Katolika.

"Mpingo [Katolika].. motsogozedwa ndi Mulungu, unaika Sunday kukhala tsiku lopembedza. Ndi mphamvu ya Mulungu yomweyo, unakhazikitsanso chiphunsitso cha kuyeretsedwa pang'ono pang'ono kwa akufa ochimwa [Purgatory] momwe unachitira ndi Sunday.' Martin Scott, Things Catholics Are asked About, 1927, p.236. (M'Jesuiti ndi mlembi).

"Mpingo wa Katolika zaka chikwi chimodzi, Umpanduko usanakhale, pogwiritsa mphamvu za utumiki wa Umulungu zopatsidwa kwa iwo, unasintha tsiku la Sabata kukhala Sunday. Koma a Mpanduko amati: 'Tingabvomereze bwanji ziphunzitso za Mpingo wopandukira Mulungu? Koma funso nlakuti,iwo alandiriranji ziphunzitso zake kuphatikiza chokana Sabata, motsutsana ndi mphunzitsi wao, Baibulo?" – The Christian Sabbath, 2nd ed., published by Catholic Mirror. (Baltimore ndi zolembera zobvomerezeka m'Chikatolika za Cardinal Gibbons.)

"Ngati mukutsatira Baibulo mwa inu nokha mungasungedi Saturday kukhala loyera, chifukwa ili ndi tsikudi limene Mulungu Wamkurukuru analamulira kuti likhale lopatulikira Ambuye." Priest F.G. Lentz, The Question Box, 1900, p.98. [Lentz [d. 1917] anali wansembe wa Chikatolika ndi mlembi, mu Illinois.)

Tsiku la Dzuwa ndi kupembedza Mulungu pa tsikuli m'malo mwa Sabata la m'Baibulo NDI CHIZINDIKIRO cha ulamuliro wa Aroma.

Anthu ambiri akanazindikira ichi! akanasiya chizindikilo cha Aroma, lemba la chirombo – ndi kubwerera kuchizindikilo chakumvera Mulungu woona – chizindikilo cha kulenganso, kuyeretsa ndi kupulumutsa.

Adzisunga Sabata..likhale pangano losatha; ndicho chizindikilo cosatha pakati pa Ine ndi ana a Israyeli; pakuti Yehova analenga zam'mwamba ndi dziko lapansi, napumula tsiku lachisanu ndi chiwiri, naonanso mphamvu." Eksodo 31:16-17.

"Muzisunga masabata anga ndithu; pakuti ndiwo chizindikilo pakati pa Ine ndi inu mwa mibadwo yanu; kuti mudziwe kuti Ine ndine Yehova wakukupatulani." Eksodo 31:13.

"Ndipo ndinawapatsanso masabata anga akhale chizindikilo pakati pa Ine ndi iwo kuti adziwe kuti Ine ndine Yehova wakuwapatula." Ezekieli 20:12.

"Muzipatulanso masabata anga, ndipo adzakhala chizindikilo pakati pa Ine ndi inu, kuti mudziwe kuti Ine ndine Yehova mulungu wanu." Ezekieli 20:20.

Ino ndi nthawi yobwerera ku chizindikilo cha Mulungu cha Kulengedwa, Kuyeretsedwa, ndi Kupulumutsidwa. Ndi nthawi yochikana chizindiklo cha Babulo wa Aroma.

"Ndiuzeni kuchokera m'Baibulo ngati nkoyenera kulilemekeza Sunday loyera. Palibe lamulo lotere m'Baibulo. Ndi lamulo la Mpingo woyera wa Akatolika!

Baibulo likuti 'Uzikumbukira tsiku la Sabata likhale loyera.' Koma Mpingo wa Katolika umati, Ndi mphamvu ya umulungu yanga ndathetsa lamulo la Sabata ndi kukulamulirani kulisunga tsiku loyamba la mulungu!

"Taonani! Dziko lonse la anthu ochangamuka liwerama mitu pansi kupereka ulemu kulamulo la Mpingo wa Katolika Woyera." Priest Thomas Enright, C.S.S.R., Mtsogoleri wa Redemptorist College, Kansas City, MO., in a lecture at Hartford Kansas, February 18, 1884, and printed in the Hartford Kansas Weekly




Call, February 22, 1884, and in the American Sentinel, New York Roman Catholic Journal, in June, 1893, p. 173.

Cardinal Gibbons anali wotchuka mu Mpingo wa Katolika ndi mneneri wa Vatican m'America, mzaka za m'ma 1900. Iye analemba bukhu lotchuka lotchedwa, Faith of Our Fathers [Chikhulupiriro Cha Atsogoleri athu] lomwe linasindikizidwa kambirimbiri.

Kalata yomwe inalembedwera ku ofesi yake inabweretsa yankho ili:

"Zoonadi, Mpingo wa Katolika ukubvomera kuti ndiwo unasintha.. NDIPO CHOKHA UNACHITACHO CHIRI KALE CHIZINDKILO cha ulamuliro wake pa za uzimu." From the Office of Cardinal Gobbons, through Chancellor H.F. Thomasi, November 11, 1895.

Zingatheke kuti munthu nkusintha kayendedwe ka masiku a pa mulungu kuyambira pa Khristu, atumwi ndiponso nthawi za Chipangano Chakale?

Werengani yankho la funso'li m'munsimu:

### *PALIBE CHASINTHIKAPO*

Anthu ambiri amati, "Kayendedwe kamasiku a pa mulungu kanasokonekera, choncho sitingathe ife kudziwa tsiku lenileni la Sabata." Koma oterowo akafunsidwa umboni wakusokonekerako amangoyankha zosamveka ndi zosokonekera.

Masiku a pa mulungu sanasokonekere, akupitirira kuyenda monga anali pa chilengedwe. Pali maumboni kuchokera m'Malemba, mbiri ya dziko, ndi sayansi. Tiyambe ndi umboni wa m'Malemba:

Kukanakhala kuti kayendedwe ka masiku a pa mulungu kanasokonekera kuyambira pa Adamu, (pomwe Sabata linakhazikitsidwa) mpaka pa Mose (pamene Mulungu anapereka Malamulo pa magome), kusokonekerako kunakonzedwa, pa Sinai pomwe Mulungu amalemba Malamulowo.

Chitsanzo cha kusasinthako ndi pa Sabata ndi kagwedwe ka manna. Kwa zaka 40 zomwe zinali milungu 2,080, Mulungu anachita chozizwa mulungu uli wonse, nalionetsa Sabata loona ka 2,080. Werengani Eksodo 16.

"Mulungu anapatsa manna mu liri lonse la masiku asanu, pa lachisanu ndi chimodzi analamulira anthu kuola miyeso ya masiku awiri. Pa tsiku lachisanu ndi chiwiri mkatewo sunagwetsedwe. Mulungu anachita ichi kuwaphunzitsa anthu ake kasungidwe koyenera ka Sabata. ANthu omwe sanafune kutsatira lamulo'li anaturuka kuti akaole mkatewu la Sabata napeza kuti panalibe, uwu. Werengani mosamalitsa Eksodo 16.

Malamulo Khumi a Mulungu akhala akutsogolera mtundu wa anthu kuyambira m'masiku a Adamu. Ndipo pa Sinai analembedwa pa tanthwe – chinthu cholimba, chokhalitsa – chosasinthika wamba kusonyeza chikhalidwe cha umyaya wa Mulungu chomwe ndi Malamulo akewo. Kutinso mwa chisomo cha Khristu, Tanthwelo, asungidwe kosatha m'mitima yathu.

Kukanakhala kuti Sabata linasokonekera ndipo kayendedwe ka masiku a m'mulungu anasintha pakati pa Mose ndi Yesu, Yesu akananena za kusinthako.

Malemba akutiuza:

"Iye [munthu] wakunena kuti akhala mwa Iye [Yesu], ayeneranso mwini wake kuyenda monga anayendera Iyeyo." 1 Yohane 2;6

M'kukhala kwake moyo pa dziko lapansi, Yesu anatisiyira chitsanzo "kuti mukalondole mapazi ake." 1 Petro 2:21.

Tilakelake ndi mtima wathu wonse kuchita monga anayendera Yesu! Moyo uchifunitsitse

"Monga chinali chizolowezi chake, [Yesu] "anasunga Sabata la tsiku la chisanu ndi chiwiri monga mwa chilamulo" (Yerekezani Lk 4:16 ndi Yoh. 15:10). Sabata linasokonekera, Yesu akanalifunafuna ndi kulibwezera kwa ophunzira ake.

Iye anauza ophunzira ake kupitiriza kusunga Sabata la m'Baibulo m'zaka za mtsogolo mwao.

"Ndipo pempherani kuti kuthawa kwanu kusakhale nyengo yachisanu kapena pa Sabata." Mateyu 24:20.

Yesu anapachikidwa pa tsiku la chisanu ndi chimodzi la mulungu lomwe lotsatiralo lake linali la Sabata (Lk 23:54-56), ophunzira ake anakonza zonunkhira kuti akadzoze thupi lake, "ndipo pa Sabata anapumula monga mwa lamulo." Luke 23:56.

Ndipo pa tsiku la Sabata la chisanu ndi chiwiri Yesu anapumula m'manda (Mateyu 28:1-7). Ndipo tsiku lotsatira Iye anauka. Tsiku lotsatira la Sabata linali loyamba la pa mulungu la ntchito, ndipo Iye anauka kupitiriza ntchito yomwe anadzera. M'mawa uja atalankhula ndi Mariya, Iye anaonekera kwa ophunzira ake kangapo pa tsiku'li (Yoh. 20:17, 19; Lk 24:13-36).

Kufikira pa imfa yake, Yesu mokhulupirirka anatisiyira chitsanzo chakumvera lamulo la Sabata. Anaphunzitsa ophunzira ake kuchita chimodzimodzi (Mat. 24:20); omwenso anasungabe Sabata pambuyo pa kuuka kwake (Lk 23:56) napitiriza kutero m'mautumiki ao (Machitidwe 13:14-16, 40-46; 16:12-15; 17:14). Iwo anamvera Mulungu osati munthu (Machitidwe 5:29), Polankhula za iye mwini ndi ife tomwe, pa za kasamalidwe ka malamulo a Mulungu, Paulo anati:

"Potero kodi lamulo tiyesa chabe mwa chikhulupiriro? Musatero ai; koma [ndi chikhulupiriro] tikhazikitsa lamulo." Aroma 3:31.

Mau a mulungu amakwanitsidwa, akuti nthawi za mtsogolo amitundunso omwe Ayuda anawasala,adzasunganso Sabata mokhulupirika (Yes. 56:3-7).

Tidzinenabe kuti Sabata linasokonekera m'nthawi ya Yesu? Tisatero, Iye anatisiyira chitsanzo chosungabe Malamulo:

### 1. KALENDA [KAWERENGEDWE KA MASIKU]

Kawerengedwe ka masiku ka Julius ndi komwe kamagwiritsidwa ntchito m'nthawi ya Khristu. Yemwe anakayambitsa, Kaisara Julius, anamwalira zaka 44 Khristu asanabadwe. Kawerengedweka komwe kanagwiritsidwa ntchito zaka mazana khumi ndi asanu, sikanali kokhoza maka pakatalikidwe ka chaka; kamatalika ndi mphindi 11 ndi masekondi 14. Apa ndi pomwe panayambira Zaka zowonjezera masiku [leap years]. M'chaka cha 1582 kunapezeka kuti tsiku la March 21 linabwezedwa m'mbuyo kufika pa March 11, kutanthauza kuti masiku khumi anachotsedwa.

Kusintha kwina koganizidwa ndi akatswiri a za m'mlengalenga [Astronomers] kunachitidwa m'nthawi ya Papa Gregory XIII; kawerengedwe kokonzedwako ndi zaka zake za masiku oonjezera kanatchedwa Kalenda wa Gregory. Aka kanayamba kugwira ntchito pa Friday, 5th October, 1582. Ndipo Friday 5th'lo linasinthidwa kukhala Friday 15th. Ichi chinapangitsa kuti mwezi wina wake ukhale ndi masiku khumi operewera – koma kutalika kwa milungu yake sikunakhuzidwe. Zinatero chifukwa chakuti masiku a mwezi kapena chaka samakhuza masiku a pa mulungu. Choncho palibe chinasokoneza kayendedwe ka masiku a pa mulungu monga mwa chilengedwe chao.

Anthu a ku Spain omwe anagona pa Thursday October 4, podzuka Friday m'mawa anangouzidwa kuti afika pa 15th. Mafuko ena anayamba kugwiritsa ntchito kalenda ya tsopanoyi nthawi yomweyo. Awa anali Spain, Portugal, ndi Italy. Mbali ina ya Germany inatsanzira kusinthaku m'1583 ndipo dziko lonse linayembekezera mpaka 1700. Mu nthawi imeneyi maiko a Netherlands, Sweden, ndi Denmark anaibvomeranso. Ndipo kotsirizira, m'1752 dziko la England ndi maiko ena omwe anali pansi pa ulamuliro wake anasinthanso.

M'October 1582, Portugal, Spain, ndi Italy anailandiranso kalenda yatsopanoyi ndi zaka zake za masiku oonjezera.

Ichi chinatanthauza kuti, mapfuko atatu a ku Ulayawa anali ndi kalenda yochepetsedwa ndi masiku khumi chaka chimenecho kusiyana ndi anzao.

Komatu zonsezi sizinasinthe kayendedwe ka masiku a mulungu ngakhale amitundu anakhala akusintha makalenda ao!

Pakati pa zaka za 1582 ndi 1752 – mpaka 1919, - mapfuko onse a ku Ulaya anasintha nayamba kugwiritsa ntchito kalenda yatsopanoyo. Koma m'zaka zonse 337 pfuko liri lonse linawerenga masiku a pa mulungu monga anali pa chilengedwe.

M'September 1752, dziko la England linalowa nao m'kalenda yatsopanoyo. Kutanthauza kuti pfuko lotchukali linali ndi chaka choperewera masiku khumi ndi limodzi poyerekeza ndi mapfuko enawo.

Koma m'zaka zonsezo,ndi za kutsogolo zakusokonekera kwa makalendaku, - pfuko liri lonse silinasinthe kayendedwe kachilengedwe ka masiku a mu mulungu.

Pa nthawi imene dziko la England limayamba kugwiritsa ntchito kalenda yatsopanoyi, masiku khumi ndi limodzi ndiwo anasinthidwa m'malo mwa khumi. Wednesday, September 2, linatsatidwa ndi Thursday, September 14. Russia ndi Greece anapitiriza kugwiritsa ntchito kalenda yakale – ya Kaisara Kulius – kwa zaka zana limodzi ndi makumi asanu zina! Kumapeto, m'1917 (Turkey), 1918 (Russia), 1919 (Serbia), ndi 1923 (Greece) – anailandira kalendayi! Panadutsa zaka 341 kuyambira pomwe kusintha kalenda'ku kunayamba.

Kwa zaka mazana atatu, makalenda anakhala osakanikira, ndipo masiku a miyezi anasiyana kuchokera dziko lina kufika ku linzake. Koma masiku a pa mulungu anakhalabe omwewo; osasintha. Likakhala Monday ku Russia linalinso Monday ku Germany, England ndi Italy ngakhale amagwiritsa ntchito makalenda osiyana. M'zaka za mazana makumi awiri, la Sabata ku Russia limakhalanso la Sabata ku England - ngakhale panali kusiyana kwa masiku khumi.

Bukhu Lomasulira Mau [Encyclopedia Britannica] limakufotokoza kufanana masikuku "masiku a pa mulungu osasinthika"; chifukwa kayendedwe ka masikuwa sanakhuzidwe ndi kusinthidwa kwa makalenda.

Mulungu [week] wa masiku-asanu ndi awiri, unaperekedwawo ndi Mulungu ku mtundu wa anthu pa chilengedwe, sunakhuzidwe ndi kusintha kwa mtundu kuli konse kufikira lero.

Chiyaninso chomwe chikutitsimikizira kuti kayendedwe ka masiku a mulungu



ndiponso Sabata sizinasinthike?

## 2. MTUNDU WA AYUDA

Atate wakumwamba watipatsa chitsimikizo china chokhazikika chakuti kayendedwe ka masiku a pa mulungu kuphatikiza la Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri sizinasinthike, - mtundu wa Ayuda.

Mitundu ina yonse ya maiko akum'mawa inatha: Ahiti, Asumeri, Ababulo, Asiriya, Amoabu, Afilisti – onse kulibe. Koma Ayuda alipo – ndipo akusungabe tsiku la Sabata lachisanu ndi chiwiri.

Padutsa zaka 3,400 kuyambira pamene Mulungu anawapatsa manna m'chipululu ndi kuwauza kulisunga Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri m'lomwe manna sanapatsidwa. Ndipo kuyambira nthawiyo, iwo anasunga la Sabata – mulungu pambuyo pa mulungu unzake, mwezi pambuyo pa unzake, chaka pambuyo pa chaka chinzake ndi m'badwo kufika mbadwo wina. Kuonjezera apo, pomwe Khristu anali pansi pano anasunga Sabata la m'Baibulo, nakhalanso chitsanzo chathu.

Kunena mosabisa si Ayuda ndi Akhristu okha omwe asunga Sabata la tsiku la chisanu ndi chiwiri m'zaka zikwi ziwiri zapitazi, komanso anthu osunga Sunday akhala akusunganso chidziwitso cha tsiku la Sabata.

Iwo amati: 1 – TIKUDZIWA kuti Yesu Khristu anasunga tsiku lolondola la Sabata lopatulika la m'Baibulo, ndipo Iye ndi chitsanzo chathu mzinthu zonse. 2 – TIKUDZIWA kuti Tsiku lachisanu ndi chiwiri la pa mulungu liriko lero'li ndi lomwe lija linalipo pomwe Yesu anali pa dziko pano.

## 3. ZOLEMBERA ZA MBIRI NDI SAYANSI

Alembi a mbiri ya dziko akupereka maumboni ochuruka kuyambira zaka zikwizikwi za m'mbuyomu. Zolembera zao zikuti anthu akhala akusunga tsiku lachisanu ndi chiwiri kukhala lopatulika kuyambira kalekale.

Akatswiri a za m'mlengalenga [Astronomers] ali ndi zolembera zolondora kwambiri za nthawi. Izi zimati, ngati kutakhala kuti zolembera zonse za nthawi zangotaika mwa ngozi, Akatswiri a za m'Mlengalengawa angathe kuzipezanso mosabvuta pogwiritsa ntchito kawerengedwe kanyenyezi ndi mayendedwe ake. Mulungu anaika nyenyezi m'mlengalenga zikhale "zizindikiro, ndi nyengo, ndi masiku, ndi zaka." Genesis 1:14. Kuonjezera pa zonsezi tiri ndi makalenda. Monsemo mulibe umboni wakuti "nthawi zinasinthika." Maumboni ena ogwirizanika ndi a m'mabuku a chidziwitso cha zinthu zonse [encyclopedias]. Iwonsi amatsimikizitsa kuti masiku a mulungu ali chikhalire monga pachilengedwe.

## 4. ZILANKHULO ZA ANTHU

M'zilankhulo 108 za 160 za mtundu wa anthu – tsiku la chisanu ndi chiwiri (Saturday) – limatchedwabe "Sabata."

Chifukwa kuyambira pachilengedwe, anthu ankadziwa kuti Sabata loona lakhala liri Tsiku la chisanu ndi chiwiri. Werengani m'mbukhu lomasulira mau la chi-Spain, mupeza kuti liu, "Sabbado" lochokera ku la chi-Latin "Subitem," lomwenso likuchokera ku chi-Hebri lothanthauza "Sabata."

## 5. A SAYANSI/MBIRI AKUGWIRIZANA

"Mulungu wa masiku asanu ndi awiri wakhala ulipo monga nthawi yoikika zaka zosawerengeka." - Anders Donner, "The Report," p. 51. (Donner wakhala ali Mphunzitsi wamkuru wa Astronomy ku University ya Helsingfors.)

"Ndakhala ndikukaikira ngati kayendedwe ka mulungu kanasinthika, komwe ndi kachikalire kwa asayansi kuyambira nthawi zosayamba." – Edouard Baillaud, "The Report," p. 52. (Baillaud anali Mkuru wa Paris Observatory.)

Maumboni ena a Asayansi ndi a Mbiri odziwika bwino ndi awa:

"Mulungu [week] ndi nthawi ya masiku asanu ndi awiri..Wakhala ulipo kuyambira nthawi zosayamba, m'maiko onse." – The Encyclopedia Britannica, 11th edition, Vol. 4, p. 988, article, "Calendar."

Poyankha Funso (1) - ..Takhala tikufufuza zotsatira za akatswiri akayezedwe ka nthawi [Chronology], koma sitinapeze kuti kayendedwe ka mulungu wa masiku asanu ndi awiri kanaliko Chikhristu chisanadze, kanasintha.

Poyankha Funso (2) – Palibe kusintha kuli konse kwa kalenda yathu kunasokoneza kayendedwe ka masiku a pa mulungu." James Robertson, Personal Letter, dated march March 12, 1932. (Dr Robertson anali Mkuru wa American Ephemeris, Navy department, U.S. Naval Observatory, Washington, D.C.)

"Momwe ndikudziwira, kusintha kwa makalenda sikunapangitse kusintha kuli konse kwa kagawo kali konse ka mulungu, womwe unalengedwa kalewo." F.W. Dyson, Personal Letter, dated March 4, 1932. (Dr Dyson anali Astronomer Royal, Royal Observatory, Greewich, London.)

"Ena a (Ayuda ndi Akhristu ) akuubvomereza kuti mulungu unalengedwa ndi Mulungu, ndipo nkuchimwa kuyesera kuusintha; koma anthu ena mosaganizira bwino, akupitirizabe kuchita motsutsana ndi chikhazikitso cha zoikikazo ngati njira yotherana ndi m'mbandakucha wa mbiri ya dziko." – Our Astronomical Column, Nature, London, No. 127, June 6, 1931, p. 869.

"Mulungu wa masiku asanu ndi awiri wakhala ulipo kuyambira masiku a Mose, choncho palibe chifukwa choupezera zifukwa lero chifukwa wakhala akuyenda mosinthana ndi inzake kuchoka mulungu wina kufika unzake ndipo masiku ake akhala akuteronso kuyambira kale mpaka lero." Dr W.W. Campbell, Statement. (Dr Campbell anali mkuru wa Lick Observatory, Mt Hamilton, California.)

"Kwa zaka zoposa 3,000 sayansi yakhala ikuyang'ana za m'mbuyo, ndipo m'kufufuza mwakuya, yapeza kuti, kutalika kwa tsiku sikunasinthe ndi kamphindi kochepetsetsa komwe." – General O.M. Mitchell, Astronomy of the Bible, p. 235.

"Pakufufuzitsa za kayendedwe ka za m'mwamba, zatsimikizika kuti palibe nthawi imene yasinthika chifukwa masiku a pa chilengedwe ndi omwe aja asanu ndi awiri, liri lonse lokhala ndi maora makumi awiri ndi anai." – Dr Hinkley, The Watchman, July, 1926. (Dr Hinkley anali m'Astronomer Wotchuka theka la zaka zana zapitazo.)

"Ngakhale pakhala pali kuipunganiza kalenda, chodziwika ndi chakuti mtundu wa anthu sunasokoneze kawerengedwe ka masiku [asanu ndi awiri] a pa mulungu kuphatikiza la Sabata kuyambira pa Adamu mpaka lero, ndi ku mibadwo yonse." – Dr Totten, Statement. (Dr Totten wa ku New Haven, Connecticut, anali mphunzitsi wamkuru wa Astronomy pa Yale University pamwe amalemba tikuwerengazi.)

"Pokhala woyang'nira nthawi ku Greenwich [England Observatory] kwa zaka zambiri, ndikuchitira umboni...kuti masiku athu onse ali m'chisamaliro cha Mulungu - oyezedwa nthawi zonse ndi kuzungulira kwa dziko m'njira yake. Kuzungulira kumeneku sikumasintha. Ndipo chaka chikupangidwa ndi masiku osaphophonya m'chiwerengero chao. Kutanthauza kuli kuyambira Pachilengedwe, palibe tsiku ndi limodzi lasokonekerapo chifukwa chakusinthasintha kwa kalenda, palibe kusokonekera kwa kayendedwe ka masiku a mulungu." – Frank Jeffries, Statement. (Dr Jeffries anali mkuru wa Royal Astronomical Society, and wa Royal Observatory Greenwich, England.)

Sabata la m'Baibulo ndi tanthwe lolimba. Linapatsidwa kwa ife ndi Mulungu pachilengedwe. Lidzasungidwa ndi opulumutsidwa m'Dziko Latsopano. (Yesaya 66:22-23).

Tikukhala m'ora lotsiriza la dziko lapansi, chinthu chomwe tisamachiwale. Ali yense payekha ali ndi udindo wakusankha la Sabata kapena Sunday. Chifukwa chimaliziro chayandikitsa.

## *KUYANDIKITSA KWA CHIMALIZIRO*

Takhala tikumva zakale. Pano timve za nthawi ino – ndi zamtsogolo.

M'zaka za mazana asanu ndi limodzi B.C, mneneri Danieli anaonetsedwa, m'masomphenya, ulamuliro woopsya womwe udzayesetse kuononga anthu a Mulungu ndi Malamulo ake.

"Nidzanena mau akutsutsana ndi Wam'mwambamwamba, nidzalemetsa opatulika a Wam'mwambamwamba, nidzayesa kusintha nthawizo ndi chilamulo." Dan. 7:25.

Chenjezo lotsutsana ndi m'chitidwewu liri pa Chibvumbulutso 14. Uwu ndi uthenga wa m'magawo atatu wolichenjeza dziko lapansi m'masiku otsiriza ano (Chibv. 14:6-12). Ndipo ukuperekedwa pafupi penipeni pakubwera Kwachiwiri kwa Khristu (Chibv. 14:14). Uthengawu ukonzetsera onse obvomera kukomana ndi Mlengi wao m'mtendere pamene akubweranso Iye.

M'chiphiphiritso ukutchedwa uthenga wa angelo atatu ouluka pakati pa mlengalenga, kuonetsa kufunikira kwake. M'uthenga wa mngelo woyamba wa Chibv. 14:6-7 anthu akuuzidwa, "opani Mulungu, mpatseni ulemelero," komanso kumpembedza Iye monga Mlengi wa miyamba ndi dziko. Anthu angachite ichi pakumvera malamulo a Mulungu.

"Opa Mulungu, musunge malamulo ake; pakuti choyenera anthu onse ndi ichi." Mlal. 12:13.

Popanda kumvera malamulo a Mulungu, palibe kupembedza kokondweretsa Mulungu.

"Pakuti ichi ndi chikondi cha Mulungu, kuti tisunge malamul;o ake." 1 Yoh. 5;3.

"Wopewetsa khutu lake kuti asamve chilamulo, ngakhale pemphero lake linyansa." Miyambo 28:9.

Ntchito yakupembedza Mulungu idalira pakumvetsetsa kuti ali Mlengi. Tiri ndi moyo chifukwa cha iye. Choncho Iye ayenera kupembedzedwa ndi kumveredwa. Kupembedza cholengedwa ndiko kuchipanga icho fano.

"Pakuti milungu yonse ya mitundu ya anthu ndiyo mafano." Mas. 96:5.

"Tiyeni, tipembedze tiwerame; tigwade pamaso pa Yehove, amene anatilenga." Mas. 95:6.

"Muyenera inu, Ambuye wathu, ndi Mulungu wathu, kulandira ulemelero ndi ulemu ndi mphamvu; chifukwa mudalenga zonse." Chibv. 4:11.

M'Chibvumbulutso 14, anthu akuitanidwa kupembedza Mlengi; angachite ichi ndi okhawo akusunga malamulo ake.

"Ndipo anawatsata mngelo wina,

wachitatu, nanena ndi mau akuru, Ngati wina alambira chirombocho, ndi fano lake, nalandira lemba pamphumi pake, iyenso adzamwako ku vinyo wa mkwiyo wa Mulungu wosasanganiza…

"Pano pali chipirirocha oyera mtima, cha iwo akusunga malamulo a Mulungu, ndi chikhulupiriro cha Yesu." Chibv. 14:9-10,12.

Mosiyana ndi olandira lemba, pali osankhidwa kumvera malamulo a Mulungu. Limodzi la malamulo amenewo – ndi lachinai – lomwe lakuti Mulungu ndi Mlengi (Eks. 20:8-11).

Kusunga lamuloli kumationetsa kuti ndife ake a Mulungu. Ndi "chizindikilo..kuti mudziwe kuti Ine ndine Yehova Mulungu wanu" Ezekieli 20:20. Limamuonetsa Mlengi wathu. "Ndicho chizindikilo..pakuti Yehova analenga zam'mwamba ndi dziko lapansi masiku asanu ndi limodzi, napumula tsiku lachisanu ndi chiwiri, naonanso mphamvu." Eks. 31:17.

" Sabata ndi chikumbutso cha chilengedwe komanso chakuti tiyenera kumpembedzera Mulungu. Liri maziko a chipembedzo choona, ndi kutiphunzitsa choonadi m'njira yomwe palibe lamulo lina lingatero." John N. Andrews, History of the Sabbath, pp 515.

Mulungu analikhazikitsa Sabata m'Edeni monga njira yosungira choondi m'maganizo a anthu; pokhala Iye Mlengi kwa myaya ifenso tipitirize kumpembedza, chifukwa Sabata nalo lipitiriza kukhala chizindikilo ndi chikumbutso chamyaya.

Uthenga wa mngelo woyamba wa Chibvumbulutso 14 ukuitanira anthu kukupembedza Mlengi. (Chibv. 14:6-7).

Uthenga wa mngelo wachitatu ukutiitanira kusunga "malamulo a Mulungu ndi chikhulupiriro cha Yesu (Chibv. 14:14:12). Ukuti onse okana kutero adzalandira chizindikiro cha chirombo (Chibv. 14:9-11).

Kodi ziphiphiritsozi zikuimira chiyani? "Chirombo," "fano," ndi "chizindikiro"?

"Zizindikirozi zayambira pa ulosi wa Chibvumbulutso 12 wa chinjoka chomwe chinafuna kumuononga Khristu pa kubadwa kwake. Chinjoka ndi Satana (Chibv. 12:9); chifukwa ndiye anatuma anthu kuti amuphe Mpulumutsiyo. Mtumiki wakuru amene Satanayo anawagwiritsa ntchito pa nkhondo yolimbana ndi Khristu ndi olungama ake, m'masiku oyambirira a mpingo wa chikhristu, unali Ufumu wa Aroma Wachikunja. Kumbali ina Chinjoka chikuimira Satana, komanso ina, ndi chiphiphiritso kuimira Ufumu wa Aroma Wachikunja.

M'Chibvumbulutso 13:1-10 chirombo china "chinafanana ndi nyalugwe" kwa ichi chinjoka chinapereka "mphamvu yake, ndi mpando wachifumu wake ndi ulamuliro waukuru" (Chibv. 13:2). Ampanduko akhala akumasulira ulamulirowu kuti ndi upapa, ufumu womwe unalandira mpando wachifumu ndi ulamuliro zomwe zinali za Ufumu wa Aroma Wachikunja.

"Ndipo chinapatsidwa icho mkamwa molankhula zazikuru ndi zamwano..Ndipo chinatsegula pakamwa pake kunena zamwano pa Mulungu, kuchitira mwano dzina lake, ndi chihema chake, ndi iwo akukhala m'Mwamba. Ndipo anachipatsa icho kuchita nkhondo ndi oyera mtima, ndi kuwalaka; ndipo anachipatsa ulamuliro wa pa pfuko liri lonse, ndi anthu, ndi manenedwe, ndi mitundu." Chibv. 13:5-7.

Ulosi'wu ukunena za chinthu chimodzimodzi: nyanga yaying'ono ya ulosi wa Danieli 7, yomwe ndi upapa.

"Ndipo chinapatsidwa ulamuliro wakutero miyezi makumi anai ndi iwiri." Chibv. 13:5. Mneneriyu akupitiriza kufotokoza, "Ndipo umodzi wa mitu yake unakhala ngati unalasidwa kufikira ku imfa." Chibv. 13:3.

"Ngati munthu alinga kundende, kundende adzamuka: munthu akapha ndi lupanga, ayenera iye kuphedwa nalo lupanga." Chibv. 1310.

Miyezi makumi anai ndi iwiri ndi chimodzimodzi "nthawi ndi nthawi zina ndi nthawi ya nusu," – zaka zitau ndi theka, kapena masiku [zaka] 1,260 za Dan. 7:25 ndi Chibv. 12:6. Iyi ndi nthawi imene ulamuliro wa upapa unazunza anthu a Mulungu. Inayamba ndi kukhazikitsidwa kwa ufumu wa upapawo m'A.D. 538, ndikutha m'1798 pomwe papa anatengedwa undende ndi ankhondo a chi-French; ndipo pakutero upapawo unalandira bala la kuimfa, kukwaniritsa ulosi: "Ngati munthu alinga kundende, kundende adzamuka."

Pa mutu womwewu, chirombo china chikufotokozedwanso:

"Ndipo ndinaona chirombo china chirikuturuka pansi; ndipo chinali nazo nyanga ziwiri ngati za mwana wa nkhosa." Chibv. 13:11.

Maonekedwe achirombochi ndi madzedwe ake ndi a pfuko losiyana ndi omwe analamulira pachiyambi. Maufumu akuruakuru a pachiyambi anaonetsedwa kwa mneneri Danieli moga zirombo zolusa, zomwe anati, ndi "mphepo zinai za mumlengalenga zinabuka pa nyanja yaikuru." Dan. 7:2.

M'Chibvumbulutso 17:15, mngelo anati madzi amaimira, "makamu, ndi mitundu, ndi manenedwe." Mphepo zinai za mumlengalenga zolimbana pa nyanja yaikuru, zikuimira nkhondo zoopsya zakulimbana kuti ufumu uli wonse ulamulire.

Koma chirombo chamaonekedwe ngati nyanga za nkhosa, chinaonetsedwa "chirikuturuka pansi" (Chibv. 13:11). Sichinaturuka m'mapfuko olimbana monga Maufumu Oyamba.

Ndi pfuko liti lomwe m'1798 linayamba kukula mphamvu, nilikhala lalikuru ku dziko lonse? America Wamgwirizano.

"Ndipo chinalankhula ngati chinjoka. Ndipo chichita ulamuliro wonse wa chirombo choyamba pamaso pake. Ndipo chilambiritsa dziko ndi iwo akukhala mommwemo chirombo choyamba, chimene bala lake la kuimfa lidapola...ndi kunena kwa iwo akukhala pa dziko, kuti apange fano la chirombo, chimene chinali nalo bala la lupanga nichinakhalanso ndi moyo." Chibv. 13:12,14.

Maonekedwe angati a nkhosa ndi malankhulidwe ngati chinjoka ndi zinthu ziwiri zotsutsana. Poyamba ndi ufumu wopanda nkhanza koma kumapeto udzazunza oyera mtima. Udzakhala wokakamiza zinthu zolakwika monga unachitira upapa. Chirombo cha nyanga ziwiri "chilambiritsa dziko ndi iwo akukhala momwemo chirombo choyamba."

Machitidwe oipa a ulamuliro wa America wa Mgwirizano adzatsutsana kotheratu ndi malamulo a ulamulirowu, omwe muli magawo atatu okhala ndi malonjezano a Ufulu Wa Munthu komanso malamulo oyendetsera dziko'lo. Atate a pfukoli anaonetsetsa kuti pasakhale kulowererana pakati pa ndale ndi chipembedzo. Ndipo malamulo oyendetsera dziko'li amatidi: "Nyuamba ya Malamulo isapange lamulo lokhuza kakhazikitsidwe ka chipembedzo, kapena oletsa ufulu wakupembedza," ndi kuti "munthu asalembedwe ntchito mdi boma potengera chipembedzo chomwe ali m' United States." Kuswedwa kuli konse kwa malamulowa, ndi komwe kungapangitse kuti chipembedzo chiri chonse chiumirizidwe chochita ndi malamulo a dziko.

Fano la chirombo choyamba lidzakhazikitsidwa ndi ulamuliro uwu:

"Ndikunena kwa iwo akukhala padziko, kuti apange fano la chirombocho." Chibv. 13:14.

"Opanga" malamulo mphamvu yao ili mwa anthu mu ulamuliro wamaonekedwe a nkhosawu. Koma 'fano lachirombo" ndi chiyani? Ndipo lapangidwa bwanji?

Kuti timvetsetse chomwe fano liri, nkofunika kuzindikira makhalidwe a chirombo choyamba – upapa.

Pamene mpingo woyamba unasokera pochoka m'ziphunzitso za uthenga wabwino nulora maphunzitso miyambo za chikunja, unadzilekanitsa ndi Mulungu. Unatembenukira ku ulamuliro wa dziko kuuthandiza kukwanitsa zofuna zake. Chipatso chake chinali ulamuliro wa upapa. Uwu unadzitengera mphamvu za dziko kwa zaka zoposa chikwi ndi kuzigwiritsa izi ntchito kuzunza "otsutsana nao" – nuubweretsa nyengo za mdima ndi chisoni ponse ponse.

Kuti fano la chirombo lipangidwe, chipembedzo chiyeneranso kukhala ndi mphamvu pa maulamuliro a dziko. Utangopatsidwa mphamvu, mpingo wa Aroma unazunza olungama. Mipingo ya Mpanduko, m'Ulaya ndi England, inachitanso chomwecho. M'zaka mazana khumi, asanu ndi limodzi ndi mazana khumi, asanu ndi awiri, zikwizikwi za abusa ndi owatsatira anakanawo chisalungamo anathamangitsidwa m'mipingo yao, nalipitsidwa chindapusa, kuponyedwa mndende, ndi kuphedwa. Paulo analosera mu 2 Atesalonika 2:3 kuti mgwirizano wa chipembedzo ndi ndalewu uchitikanso m'masiku otsiriza.

Kusiyana pa ziphunzitso kwa mipingo ya Mpanduko kuli chitsimikizo kuti sipangakhalenso chikondi pakati pao. Kudzakhala magwero okakamiza munthu ali yense ku zofuna zao.

Monga mwa ulosi wa Baibulo, pamene mipingo yaikuru ya United States, idzagwirizana pa ziphunzitso zomwe ndi zofananirako, idzakakamiza ulamuliro wa dziko kukhazikitsa malamulo okakamiza anthu onse kubvomereza zofuna zao, pakutero America wa Mpanduko adzapanga fano la ulamuliro wa Aroma, pomwepo chizunzo cha olungama chidzayamba.

Chirombo cha nyanga ziwiri chidzapangitsa anthu kulandira chizindikilo:

"Ndipo chichita kuti onse, ang'ono ndi akuru, achuma ndi osauka, ndi mfulu ndi akapolo, alandire chilembo pa dzanja lao ndi pamphumi pao; ndi kuti munthu sangakhoze kugula kapena kugulitsa, koma iye yekha wakukhala nacho chilembo, ndilo dzina la chirombo, kapena chiwerengero cha dzina lake." Chibv. 13:16-17.

M'mutu wotsatira, timva za chenjezo la mngelo wachitatu lomwe likuti:

"Ndipo ngati wina alambira chirombocho, ndi fano lake, nalandira lemba pamphumi pake, kapena pa dzanja lake, iyenso adzamwako ku vinyo wa mkwiyo wa Mulungu." Chibv. 14:9-10.

"Chirombo,"chadzapembedzedwa mokakamizachi ndi mgwirizano wa cha nyanga ziwiri ndi upapa chibv. 13.

Nanga "fano la chirombo" ndi chiyani?

"Fano la chirombocho" ndi mgwirizano womwe uchitike pophatikizana chipembedzo [mipingo] ndi maulamuliro a dziko momwe chipembedzocho chidzafuna mphamvu za maulamuliro adzikowo kukakamiza ziphunzitso zake zolakwika.

Utangochenjeza za kuopsa kwa kupembedza chirombo, ndi fano lake, ndi chizindikilo chake, ulosi ukuti:

"Pano pali chipiriro cha iwo akusunga malamulo a Mulungu, ndi chikhulupiriro cha Yesu." Chibv. 14:12.

Osunga malamulo a Mulungu akulekanitsidwa ndi opembedza chirombo, fano lake, ndi kulandira chizindikilo chake. Gulu lina lidzamvera Mulungu pomwe lina lidzakana kutero.

Makhalidwe a chirombo ndi a fano lake adziwika potsutsana ndi malamulo a Mulungu:

"Nidzayesa kusintha nthawizo ndi chilamulo." Dan. 7:25.

# CHIYANI CHIDZAPANGITSE ANTHU OCHURUKITSA KUSALOWA KUMWAMBA

Paulo anaufotokoza ulamuliro wopandukirawu "munthu wosayeruzika" wodzikweza pa zonse zotchedwa Mulungu.

"Munthu asakunyengeni konseko; kuti silifika, koma chiyambe chifike chipatukocho, nabvumbulutsidwe munthu wosayeruzika, mwana wachiononongeko, amene atsutsana nazo, nadzikuza pa zonse zotchedwa Mulungu, kapena zopembedzeka; kotero kuti iye wakhala pansi ku Kachisi wa Mulungu, nadzionetsera yekha kuti ali Mulungu." 2 Ates 2:3-4.

Pakusintha malamulo a Mulungu upapa wadzikweza kuposa Mulungu. – Yense wakusunga malamulo osinthidwawo akulemekeza wowasintha. Kumvera malamulo a upapa m'malo mwa Mulungu ndi kulandira "chizindikilo cha chirombo."

M'chizunzo chirinkudza, opembedza Mulungu adzadziwika pakusunga lamulo lachinai; lomwe ndi chizindikilo cha mphamvu yake yakulenga ndi kupulumutsa. Opembedza chirombo adzadziwika ndi sabata la Aroma – lopatulikira upapa.

Khristu sanasinthe tsiku la Sabata werengani chodzikanira chake (Mat.5:17-19). A Mpanduko, akutsimikiziranso kuti palibe m'Malemba za kusintha Sabata. Mpingo wa Katolika umabvomera kuti unasintha la Sabata kulika Sunday, ndipo a Mpanduko akamasunga Sunday kulemekeza ulamuliro wa Mpingowo.

"..alembi a upapa akubvomereza kuti kusintha la Sabata kukhala Sunday, ndi chinthu chomwe Ampanduko akubvomerezana nacho;..posunga Sunday, iwo akubvomereza mphamvu yomwe mpingo uli nayo yosintha zikondwerero, ndi kulamulira zichitike ngakhale m'njira ya uchimo." Henry Tuberville, "An Abridgenent of the Christian Doctrine," p.58.

"Kusungidwa kwa Sunday ndi Ampanduko .. ndi ulemu womwe akupereka, ku ulamuliro wa [Katolika] Mpingo, ." Plain Talk About Protestantism, p. 213.

Pogwirizana ndi maulamuliro a dziko kukakamiza chipembedzo chachikunja, mipingo ipanga fano la chirombo. Kukakamiza lamulo la Sunday kwa pfuko la United States kuli kukakamiza chipembedzo cha chirombo ndi fano lake.

Onse amene anasunga Sunday, poganiza kuti akusunga la Sabata la m'Baibulo, kuphatikiza aKatolika, omwe akutero moona mtima. Mulungu akuwalandira awa mukusadziwa kwao komweko.

Kuyambira pomwe Sunday likhale lokakamizidwa mwa lamulo, ndipo munthu adzazindikira za kusiyana kwake ndi Sabata loona, yense wonyozera lamulo la Mulungu, ndi kusunga lamulo la Aromali, - Adzapembedza chirombo ndi fano lake – ndipo pomwepo anthuwo adzalandira "chizindikiro cha chirombo."

Uthenga wa mngelo wachitatu a Chibvumbulutso 14:9-12 ndi chenjezo ku dziko lonse. Anthu afikilidwe chisanafike chiweruzo chotsiriza cha Mulungu pa dziko lapansi.

Monga mngelo woyamba akulalikira ku, "mtundu uli wonse ndi pfuko ndi manenedwe ndi anthu" Chibv. 14:6, Chomwechonso uthenga wa mngelo wachitatu kudziko lonse. Ulalikidwe ndi mau opfuula, ndi mngelo wakuuluka pakatikati pa mlengalenga; kutanthauza uperekedwe mwamphamvu ndi momveka pa dziko lonse.

M'kati mwa kulimbana, magulu a Chikhristu adzagawidwa pawiri – gulu losunga malamulo a Mulungu ndi chikhulupiriro cha Yesu, ndi lolambira chirombo, fano lake ndi kulandira chizindikilo chake. Ngakhale Mpingo udzagwirizane ndi ulamuliro wa dziko kukakamiza anthu onse, "ang'ono ndi akuru, achuma ndi osauka, ndi mfulu ndi akapolo"kuti alandire "chilembo/chizindikilo cha chirombo" (Chibv. 13:16), anthu a Mulungu adzakanitsitsa kuchilandira ichi.

Yohane, m'masomphenya , anaonetsedwa gulu la "iwo amene anachilaka chirombocho, fano lake ndi chiwerengero cha dzina lake, akuimirira pa nyanja ya mandala, nakhala nao azeze a Mulungu. Ndipo aimba nyimbo ya Mose mtumiki wa Mulungu, ndi nyimbo ya Mwanawankhosa" (Chibv. 15:2-3).

Baibulo ndi mbiri yadziko zikutsimikiza kuti Mulungu sanasinthe la Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri.

Mpingo wa Aroma, umatinso ndi anthu ochepetsesa omwe akusunga Sabata la Mulungu la m'Baibulo:

"Mpingo [Katolika] unasintha Sabata kuliika pa Sunday pogwiritsa ntchito ulamuliro wa umulungu, wamyaya wopatsidwa kwa iwo ndi mutu [wa Mpingo], Yesu Khristu. Choncho Ampanduko omwe amati Baibulo ndi maziko okhawo a chikhulupiriro chao, sayenera kusunga Sunday. Ndi a Seventhday Adventist okha omwe ndi Ampanduko okhazikika."The Catholic Universe Bulletin, August 14, 1942, p.4. (Nyuzi ya pa mulungu ya Cleveland Diocese ya chi-Katolika).

"Funso: - a): Baibulo limati, 'Sabata la tsiku lachisanu ndi chiwiri ndi lakupumula la Yehova lomwe Iye analipatula. Nanga sabata la Sunday linadza bwanji? (b) Ndiye kuti ma-Adventist akulondora posunga tsiku'li?

"Yankho: Ngati mumadalira Baibulo lokha sungani Saturday kukhala loyera, chifukwa ndi lomwe Mulungu Wam'mwambamwamba analipatula. Posunga Sunday, onse omwe si-Akatolika akungotsatira miyambo ya Mpingo wa Katolika kwa zaka 1,800. Chobwitsa nchakutiu: iwo akunyoza ulamuliro wa Mpingo [Katolika], nanga akusungiranji Sunday? Iwo amene akusunga Saturday, monga a Seventhday Adventist, akulondora… Koma ife tikuti Baibulo si maziko okhawo a chikhulupiriro chathu, timalemekezanso Miyambo ya Mpingo." – Francis George Lentz, The Question Box, 1900, pp. 98-99. (Lentz, yemwe anamawlira 1917, anali wansembe wa chi-Katolika ku Illinois).

"Funso: Kodi pali ulamuliro m'Baibulo wakuti Sabata lisinthidwe kuikidwa pa loyamba la mulungu? Nanga ndi ndani anampatsa papa ulamuliro wosintha lamulo la Mulungu'li?

Yankho: "…A Seventhday Adventist akukhoza, popitiriza kulisunga Saturday monga Ayuda..Inu simukuchiona kukhala chodabwitsa kuti anthu omwe amati, Baibulo ndi lokhalo mphunzitsi wao, akulephera kutsatira ziphunzitso zake, koma m'malo mwake akutsatira Miyambo ya Mpingo wa Katolika?" Bertrand CONWAY, The Question Box, 1903 ed., pp.254-255; 1915 ed., p.179. (Conway [1872-1959] anali wansembe wa Chipani cha Paulo mu Mpingo wa Katolika).

"A Mpanduko adayenera kusunga Saturday lopatulika ndi kuwasiyira Akatolika kusunga Sunday lao. Palibe zogonjerana apa!" Catholic Mirror, September 2 and 23, 1893. (Catholic Mirror, ya Baltimore inali zolembera zobvomerezeka za Cardinal Gibbons.)

Mpingo wa Katolika umati:

"Sunday ndi CHIZINDIKILO cha ulamuliro wathu!..Mpingo uli ndi mphamvu zoposa Baibulo ndipo kusintha kwa kasungidwe ka Sabata ndi chitsimikizo chake." The catholic Record, London, Ontario, Canada, Septenber 1, 1923.

"Pali umboni m'Baibulo kuti ndiyenera kusunga Sunday lopatulika. Sindikuupeza. Ndi lamulo loyera la Mpingo wa Katolika lokha. Baibulo limati, 'Uzikumbukira Sabata likhale lopatulika.' Mpingo wa Katolika ukuti Ai. Ndi mphamvu ya umulungu wanga ndinasintha tsiku la Sabata kukhala pa loyamba la mulungu. Ndipo taonani! Dziko lonse likumvera lamulo la Mpingo Woyera wa Katolika." Wansembe Thomas Enright, C.S.S.R. Mkuru wa Redemtionist College, Kansas City, MO., mphunziro la ku Hartford, Kansas, February 18, 1884, yofalitsidwa m' Hartford Kansas Weekly Call, February 22. 1884, and the American Sentinel, a New York Roman Catholic Journal in June 1893, pege 173.

"Zoonadi Mpingo wa Katolika umati ndiwo unakuchita kusinthako – NDIPO KULI CHIZINDIKILO cha mphamvu yake yokhala chipembedzo." – Zochokera m'Office ya Gibbons, kudzera mwa Chancellor H.F Thomas, November 11, 1895.

Sabata la m'Baibulo liri yeso lakuru lakumvera. Yesu akubwera, mayesero onse a moyo uno adzakhala nthano yakale.

Awerengi a chifupikitso ichi cha bukhu lathu Our Sunday is not Sabatth atilembere kuti tiwatumizire bukhu'li kapena makubu ochurukirapo momwe mwalembedwa motambasula bwino zomwe zafupikitsidwa pamwambazi. Lemberani ku: Harvestime Books, Altamont, TN 37301 931-692-3777. USA.

Fufuzani, Werengani, Dindani Mabukhu: www.bible-sabbath.com www.earthsfinalwarning.com www.evolution-facts.org www.present-truth.org www.worldincrisis.org www.pathlights.com www.stepstolife.org

**MUKAFUNA KUMVA NDI KUDZIWA ZAMBIRI LEMBERANI KU:**


LOUD CRY AND FAMILY LIFE MINISTRIES
P.O. BOX 2850,
BLANTYRE,
MALAWI. CENTRAL AFRICA.

RESTORATION SEVENTHDAY ADVENTIST MINISTRIES
P. O. BOX 510751,
CHIPATA,
ZAMBIA. CENTRAL AFRICA.

ADVENT PROPHECY UPDATE
P.O. BOX 70516,
NDOLA,
ZAMBIA, CENTRAL AFRICA.